

AHEBRI, MUTU

WACHISANU NDI CHIMODZI ²



...kuti tiphunzire Mawu Ake ofunika.

Ine ndinabwera muno kanthawi kapitako, ndipo ine ndinali nditanamula Mabaibulo awiri. Ndipo ine ndinali ndi kuyankhulana kwapadera pang'ono ndi dona kumbuyo kuno, ndipo ine ndinamuuza iye kuti ngati ine ndingati ndilalikire kuchokera mu onse awo, tikuyenera kukhala ndi phunziro labwino kwambiri. Koma ili ndi lexicon Yachigriki, chotero basi chinachake chimene ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mmenemu, usikuuno. N—ndi...Iko ndi kutanthauzira kwa liwu pa liwu, kuchokera mu Chigiriki chapachiyambi, kupita mu Chingerezi. Ndipo ilo lakhala liri lathandizo lochuluka kwa ine potsatira mzerewu. Ndipo ine ndikungofuna kuti ndiwerenge chinachake kuchokera mu ilo, chifukwa tsopano ife tikuphunzira mu Bukhu ili la Ahebri, ndipo ife tikungobwera tsopano ku matanthauzo akuya kwenikweni.

²¹⁹ Ndipo ine ndimamuuza M'bale Neville, maminiti angapo apitawo, “Ife tikufika mu gawo lomwe anthu azikanda mutu wawo ndi kuti, ‘Ine sindikuzikhulupirira zimenezo.’” Mukuona? Ndiwo mtundu umene ife tikufikamo. Apo ndi pamene ife timazikonda izo.

²²⁰ Mtumiki wina ananena kwa ine, iye anati, “Chabwino, ine ndikulingalira kuti pakhala kukanda mutu kochuluka.”

²²¹ Ine ndinati, “Ndi chimene ife tikufuna kuti tichite.” Mukuona?

²²² Baibulo likhoza kukhala ndi tanthauzo limodzi lokha. Ilo silingakhoze kukhala ndi matanthauzo awiri. Ndipo ngati gawo limodzi la Baibulo likunena chinthu chimodzi, ndipo gawo lina la Baibulo likunena china chakenso, ndiye chinachake chalakwika. Mukuona? Ilo liyenera kuti lizinena chinthucho, njira yonse kudutsa. Koma, kumbukirani, mu kuphunzira Baibulo, “Izo zinabisidwa kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo izo zaululidwira kwa makanda,” chifukwa izo ndi za Bukhu lauzimu.

²²³ Ndipo Ilo si bukhu lakumadzulo. Ilo ndi Bukhu lakummawa. Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chingakhoze kulitanthauzira Ilo, ndipo icho ndi Mzimu Woyera. Ine ndikudziwa kuti mmodzi aliyense wa ife akufuna anene, kuti, “Mzimu Woyera umatiuza ife zomwe ife timakhulupirira mu Ilo.” Chabwino, tsopano, ngati Lemba lirilonse lifola ndendende mofanana, ndiye umenewo ndi Mzimu Woyera. Ngati iwo

samafola, ndipo muli ndi mpata *apa*, ndi mpaka cha *apa*, ndiye pali chinachake chalakwika ndi kakhulupiriridwe kathu. Ndipo, o, Ilo ndi Bukhu lododometsa.

²²⁴ Tsopano, ine ndikufuna inu kuti muchite izi pamene ife tikuphunzira. Tsopano ife tiyenera kuti tichoke molawirira mmawa waku Wyoming, Ambuye akalola. Muzitipempherera ife.

Ndipo sabata yotsatira iyi, M'bale Graham Snelling, apa. . . Iye alipo. Ine ndinamumva iye, basi maminiti angapo apitawo, akupanga zolengeza zake. Ndipo mpingo uno uli mu chiyanjano chathunthu ndi chitsitsimutso chake. Ndipo ife tikupemphera kwa Mulungu, kuti amupatse iye chitsitsimutso chopitirira, chachikulu, mochuluka. M'bale Graham anali ndi chitsitsimutso kwa M'bale. . . komwe kuno ku Charlestown, M'bale Junior Cash, ndipo uko kunali otembenuka zana, ine ndikukhulupirira. [Winawake akuti, "Eyite-foro."—Mkonzi.] Otembenuka Eyiteforo. Chotero, kwa izo, ife tikumpatsa Mulungu matamando. Ndipo ife tikudalira kuti icho chikhala ndi mazana asanu ndi eyite foro kuno, mu malo awa kuno.

²²⁵ M'bale Graham anakomana nane lero, ndipo iye anati, "Tsopano, M'bale Bill, ine ndikutsimikiza kuti inu mukumvetsa kuti ine sindiri kuno kuti ndiyambitse ntchito ina motsutsana ndi kachisiyu, chifukwa ndine gawo la kachisiyu." Iye ali kuno basi kuti. . . Iye akumverera pa mtima wake kuti iye akufuna kuti achititse chitsitsimutso, ndipo Ambuye akumutsogolera iye kuti achite izo. N—ndipo iye akuwaitanira otembenuka, ndipo ali nawo mpingo, woti awatsanuliremo iwo kumene, "Uno ndi mpingo wa kwanu, ngati inu muti mulowemo, muti mutembenezidwe."

²²⁶ Ndipo ndi ntchito yathu, ngati Akhristu, kuti tikamuthandizire iye ndi chirichonse chomwe ife tingathe. Ndipo Ambuye amudalitse M'bale Graham. Ndipo inu muli, aliyense, mukuitanidwa mwachikondi ku msonkhano wa M'bale Graham kuntunda kuno, ndi chilolezo chathunthu kuchokera ku mpingo uwu, ndi chiyanjano chathunthu kuti tikamuthandizire iye mwanjira iliyonse yomwe ife tingathe, pofuna miyoyo yotaika ndi kwa Ufumu wa Mulungu.

²²⁷ Ambuye akudalitseni inu, M'bale Graham, akupatseni inu misonkhano yaikulu. Iye sakudziwa kuti atsiriza liti. Iye akungoyamba. Ndipo chotero, M'bale Graham wakhala namo imo monga inemwini, *mokwera* ndi *motsika* mwambiri. Umo ndi momwe moyo umayendera. Izo zimakupangitsa iwe kuyamikira *mokwera* iwe ukakhala utadutsa kale *motsika*. Ngati munthu apanga kugwa ndi kukhala pomwepo, iyeyo ndi wamantha. Ine ndimakhala ndi chidaliro pamene munthu awuka ndi kuyesa kachiwiri. Uko nkulondola. Ine ndikutsimikiza inu mukhoza

kutanthauzira zomwe ine ndikutanthauza. Tsopano, musati muiwale izo, sabata ikubwera iyi.

²²⁸ Tsopano, mu Bukhu ili la Ahebri, ife sititenga zakoyambirira usikuuno.

²²⁹ Tsopano, Lamlungu likudzali, Ambuye akalola, M'bale Neville adzalengeza. M'bale Cox pano, kapena ena a iwo, amudziwitsa iye, ngati ife titi tidzafike mu nthawi kwa msonkhano wa Lamlungu likudzalo. Iye adzazilengeza izo pa wailesi. Ndipo ife tiri . . . Inu nonse mumamvetsera ku wailesi yake tsopano, n—n—ndipo muziwaitanira oyandikana nawo anu onse kuti azimvetsera. Ine ndimasangalala kwenikweni kumvetsera ku kulalikira kwawo ndi kuimba, gulu la a Neville anai. Ine sindikunena izo chifukwa iye ali pano. Ngati ine ndikanamanena izo, ndipo nkusamatanthauza izo mu mtima mwanga, ine ndikanakhala wachinyengo. Ndiko kulondola. Ine ndikanasowa kuti ndilape. Koma ine ndikutanthauza izo. Ndipo ine kuli bwino ndimupatse iye mphukira ya duwa tsopano kusiyana ndi kudzamupatsa iye nkhatu yonse atapita kale.

²³⁰ Nthawi ina ine ndinali kuyenda ndikutuluka pakhomo, ndipo apo panali dona anabwera pafupi, ndipo iye anati, “M'bale Branham, o, momwe ine ndimakomeredwera nawo uthenga uja!”

²³¹ Ine ndinati, “Zikomo inu.” Zinandipangitsa ine kumverera bwino.

²³² Winawakenso anabwera, nati, “M'bale Branham, ine ndinakomedwa nawo Uthenga uja.”

²³³ Ine ndinati, “Zikomo inu.”

²³⁴ Uko kunali mlaliki wamng'ono kumeneko, wochokera cha kuno mu gawo lakumpoto la dzikoli, mu boma, iye anati, “Mulungu adalitsidwe, ine sindimafuna kuti anthu azibwekerera za ine monga chomwecho.”

²³⁵ Ine ndinati, “Ine ndimafuna.” Ndipo ine ndinati, “Pali kusiyana kumodzi kokha pakati pa ine ndi inu. Ine ndimakhala wouna mtima nazo.” Ndiko kulondola. Ife tonse timakonda kumva mawu abwino akunenedwera kwa ife. Ndipo i—ine ndikuganiza ndi zabwino kunena mawu abwino a izo. Ndipo ngati iwe ukufuna kuti winawake azinena mawu abwino okhudza iwe, zinena mawu ena abwino okhudza winawakenso. Umo ndi momwe mungamachitire izo, ndiye inu nthawizonse muzinena zinthu zabwino kwambiri zomwe inu mungathe zokhudza aliyense. Ndipo izo zimapangitsa gudumu kugudubuzika bwinoko.

²³⁶ Tsopano, mu izi, Lamlungu likudzali, Ambuye akalola, mwa lingaliro langa, ife tiri nazo, tizingozamira zamira mu zinsinsi zazikulu izi za Mulungu. Ife tikupita mu Melkizedeki: Yemwe

Iye anali, komwe Iye anachokera, komwe Iye anapita, zomwe zinachitika kwa Iye, ndi zonse zokhudza Melkizedeki.

²³⁷ Ndipo tsopano, Lachitatu lathali usiku, M'bale Neville anagunda pa mutu wotsirizitsa wa Umulungu wapamwamba ndi unsembe wa Ambuye wathu Yesu, zomwe zikuyambira pachiyambi, “Mulungu, mu nthawi zamakedzana ndi mmachitidwe osiyana ankayankhula kwa makolo athu mwa aneneri, mu tsiku lotsiriza lino wayankhula kwa ife kupyolera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu.”

²³⁸ Ndiye iye akupitirira nazo, ndipo akuyamba kutiuzza ndi kufanizitsa yemwe Iye anali, kumubweretsa Iye mopitirira pansi mpaka ku mutu wa 5, pa mapeto a mutu wa 5.

²³⁹ Ndiye kuyambira pa mutu wa 6, ife tinapeza izi mu phunziro lathu mmawawu.

Chotero posiyana nazo zoyambirira za chiphunzitsa cha Khristu, tiyeni ife tipite mtsogolo mpaka ku ungwiro; . . .

²⁴⁰ Ndi angati anasangalala nawo uthenga pa ungwiro? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] “Tiyeni ife tipite mtsogolo mpaka ku ungwiro.” Umenewo unali Uthenga wathu, mmawa uwu, mu mutu wa 6 wa Ahebri.

²⁴¹ Tsopano ife tikungofika pa malo pomwe ife tikuyamba kupeza g—gawo lenileni. O, ife tonse tikhoza kugwirizana pa zinthu izi: pa Umulungu wa Khristu; ndi Iye pokhala Mwana wa Mulungu; ndi momwe Iye analiri ndi Mulungu, ndipo Mulungu anali ndi Iye; ndipo Iye anali mwa Mulungu, ndi Mulungu mwa Iye, ndi zina zotero. Ife tonse timagwirizana pa zimenezo. Koma, tsopano, kuyambira apa popitirira, ine sindikudziwa momwe ife titi tigwirizanire. Chotero chirichonse chomwe izo ziri, usiku ungapo uliwonse, ife tizikupatsani inu mwayi ndipo muzindilemba ine kolemba kakang’ono ndi kundiuza ine momwe inu mukuganizira za Iwo.

²⁴² Ndiye ine ndiyenera kuti ndiyankhe mafunso. Ndipo ngati ine sindingathe kuwapeza iwo, ine ndiziti, “M'bale Neville, kodi inu mukuganiza chiani za izo?” Ine ndiziti, “Ndi uyo apo. Musiyeni iye awayankhe iwo.” [M'bale Neville akuti, “Ndi pamene ine nditi ndziwerenga Chigriki.”—Mkonzi.] Ndi pamene Iye ati aziwerenga lexiconi, kuchotsapo Chigriki. Ine ndikuganiza yakwana nthawi yoti ine nditero, nanenso.

²⁴³ Koma, tsopano, ngati ife tifike mmusi ndi kukhala owonamtima kwenikweni, ndi kudzera kwenikweni pa cholinga chimodzi, ndicho, kuti tidzaphunzire. Ine ndikufuna kuti ndiphunzire, nanenso. Ndipo Baibulo linalembedwa, anati, “Ilo liri. . . Malemba alibe kutanthauzira kwa mseri.” Izo zikutanthauza kuti Lemba liyenera lizitanthauzira Lemba. Mukuona? Lemba lililonse liyenera lizimasulira limzake, njira yonse kudutsa mu Baibulo, kuti lipange chinthu chimodzi

chachikulu. Chifukwa, Mulungu sangakhoze kusintha, chifukwa Iye ndi Mulungu wosasintha.

244 Tsopano, “Poleka . . .”

Chotero polekana nazo zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipitirire mtsogolo ku ungiro; . . .

245 Ine ndikumukonda Paulo akamanena zinthu zimenezo. Paulo sanali konse munthu yemwe anakonda kukhala motalika kwambiri pa malo amodzi. Iye anakonda kusunthira mtsogolo, mwakuyapo. Nthawi ina, mu Lemba, iye anati, “Ine, poiwala zinthu izo zomwe ziri zakale, ine ndikukankhira cha ku malo a kuitana kwapamwamba.” Mukuona? Iye amakhala akukankhirabe mtsogolo.

246 Apa iye anati:

Tsopano poiwala zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu (yemwe iye anali, chimene iye anali), tiyeni tipitirire mtsogolo ku ungiro; . . .

247 Tsopano ife, choyamba, ife timafuna kuti tipeze, “Kodi ife tingakhoze kukhala *angwiro*?” Ndipo ife tinapeza, mu Malemba mmawa uno, Mateyu 5:28, kuti Yesu ananena kuti ife “timayenera tikhale *angwiro* basi monga Mulungu analiri,” kapena ife sitikanati tikalowe umo.

248 Ndiye ife tinapeza kuti ife tinali, aliyense, “titabadwa mu tchimo, titawumbidwa mu kusaeruzika, tinabwera ku dziko kumanena bodza.” Ndipo panalibe kanthu kamodzi kolongosoka kokhudza ife, kotero ife tikanakhoza bwanji konse kukhala *angwiro*?

249 Tsopano apa pali zomwe ife tinazipeza ndiye, pa, kuwerenga, potenga Lemba ndi Lemba, kuti, “Yesu, mwa nsembe imodzi, anakhalitsa wangwiro, kwanthawizonse, Mpingo Wake.” Iye . . . Iye ndiye tiri *angwiro*, kudzera mwa Khristu. Ndipo ife tiri afulu kwa chiweruzo, kudzera mwa Khristu. Ife sitidzafa konse kudzera mwa Khristu. Ife tataya imfa ndipo tapeza Moyo, kudzera mwa Khristu; osati kudzera mu mpingo uliwonse, osati kudzera mu chipembedzo chirichonse, osati kudzera mu zopambana zirizonse, osati kudzera mu kuyankhula ndi malirime, osati kudzera mu kufuula, osati kudzera mu kudzigwedeza, osati kudzera mu kuvina mu Mzimu, koma mwa chisomo.

250 Mulungu amamuitana yemwe Iye angamufune. Ndipo zonsezo zimakhala mwa kusankha, ife tinazipeza. Ife tinapeza, kuti, “Si iye yemwe afuna kuti apulumutsidwe. Si iye yemwe akufuna kapena iye yemwe ahamanga; ndi Mulungu yemwe amasonyeza chifundo.” “Ndipo palibe munthu yemwe angadze kwa Yesu kupatula Mulungu atamukoka iye, poyamba.” Chotero kodi inu mukhala ndi chochita chiti, mulimonse? Inu

mulibe kanthu kochita nazo. Inu mwachoka pa chithunzicho, mwapalimodzi.

²⁵¹ Ife tinapeza kuti munthu samamufunafuna konse Mulungu. Ndi Mulungu amamufunafuna munthu. Ndipo ife tinapeza apo, ndiye, kuti Mulungu ali gwero lokha la Moyo Wamuyaya. Ife tinapeza kuti chirichonse chomwe chiri Chamuyaya chiribe chiyambi kapena chiribe mapeto. Chotero, ife tikupeza kuti gehena anali ndi chiyambi, ndipo ali nawo mapeto. Ndipo pali kokha... Palibe mmodzi angakhoze konse kunena kuti... Gehena ndi wa kwanthawizonse, kwanthawizonse, inde, kwanthawizonse, koma osati Wamuyaya.

²⁵² *Kwanthawizonse* ndi “danga la nthawi.” Baibulo limati, “Kwanthawizonse ndi kwanthawizonse.” Ndipo inu kayang’aneni izo ndi kukafufuza ngati *kwanthawizonse* samatanthauza “danga la nthawi.” Yona anati iye anali mu mimba ya chinsomba “kwanthawizonse.” Ndi Malemba ena ochulukwa, *kwanthawizonse* amangotanthauza “danga la nthawi.”

²⁵³ Koma, Muyaya, ndiwo kwanthawizonse, ndiwo nthawi za nthawi ndi nthawi za nthawi za nthawi. Ndiwo Muyaya. Ndipo ife tikupezapo kuti gehena si Wamuyaya, koma ndi wanthawizonse. Ndipo nchifukwa, inu muyenera kumawasamalira mawu amenewo, tsopano. Ngati inu simutero, inu mumafika posokonezedwa. Tsopano, kumbukirani, zinthu zokhazo zimene zinalibe chiyambi, ziribe mapeto. Chotero, Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo,” wanthawizonse? Kodi izo zikumveka molondola? Ayi. “Ali nawo Moyo Wamuyaya.” Ndipo mawu okuti *Wamuyaya* ndi “Mulungu.” Mawu, apa ali apa pomwe mu lexiconi Yachigriki, Zoe Moyo wa Mulungu mkati mwanu. Ndipo inu muli basi Wamuyaya momwe Mulungu aliri Wamuyaya, chifukwa inu muli ndi Mulungu mkati mwanu.

²⁵⁴ Chibadwa chanu chakale chinafa, chibadwa cha dziko, ndipo inu mumakhala cholengedwa chatsopano. Ndipo zokhumba zanu, moyo wakale uja umene unali ndi chiyambi pamene Mulungu anapumira mpweya mu mphuno zanu, pamene inu munkabadwa, moyo uwo wa chikhalidwe chachithupi unafa. Ndipo iwo unali ndi chiyambi ndipo iwo unali ndi mathero, ndipo iwo unafa ndipo anathana nawo kwanthawizonse, chibadwa chakalecho. Ndipo Mulungu anabwera mkatimo ndi Chikhalidwe chatsopano. Ndiye, chikondi, chisangalalo, mtendere, kupirira-motalika, kudekha, mtendere, chipiro, ndi kuleza, ndi chifundo, izo zinalowa umo; ndipo zinatenga malo a njiru, ndi kupsya mtima, ndi udani, n—ndi ukali, makangano, ndi zinthu zonse izo. Izo zinatenga malo ake, pamene inu munadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Inu mukumvetsa izo, mwatcheru kwenikweni, tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

255 Chotero, mvetserani. Pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya. Upezeni Iwo. Iwo uli, Mulungu yekha ali nawo Moyo Wamuyaya. Baibulo linanena chomwecho. Mulungu yekha ali nawo Moyo Wamuyaya. Ndipo ngati munthu ati akazunzike mu hade, kwanthawizonse, iye ayenera kuti akhale ndi Mulungu, Muyaya. Koma ine ndikunena kuti ilipo.

256 Tsopano, kumbukirani, ine sindikunena kuti kulibe gehena woyaka. Alipo gehena woyaka, moto ndi mwalawasulfure. “Komwe—nyongolosi ili... motowo sumazimitsika ndipo nyongolosi siimafa konse,” ya moto ndi mwalawasulfure, chilango. Izo zikhoza kudzatha zaka mabilioni zana. Koma izo ziyenera kudzakhala ndi mathero, pakuti gehena analengedwera kwa Mdierekezi ndi angelo ake. Ndipo chirichonse chomwe Mulungu yemwe, Mwiniwake, chomwe chinali pachiyambi, chirichonse chinabwera kuchokera kwa Mulungu. Pamene mzimu womwe...

257 Inu mukatenga *Mzimu* wa chikondi, uyo anali kasupe wamkulu wa Mulungu, wangwiro, wosaipitsidwa. Kuchokera pamene, kunadza chikondi *chopotozedwa*. Ndiye izo zinabwera mu chikondi *chaumunthu*. Kenako izo zinabwera mu chikondi *chogonana*. Ndiye izo zinadzafika mu zikondi zina, zikondi ndi zikondi, ndi kumangopitirira kupotozedwera mmusi mpaka zinafika pongokhala *nyansi*. Koma zinthu zonse izo zinali ndi chiyambi. Ndipo tsiku lina izo zidzathera molunjika basi kubwerera ku chapachiyambi; ndi Zamuyaya; kumene kusilira, chikondi chaumunthu, chikondi chachikhumbo, zikondi zonse izo zidzayenera kuti zidzathe.

258 Tizikhulupiriro tonse iti todzipangitsa ta Chikhulupiriro ito tidzayenera kuti tidzathe. Pali Chikhulupiriro choona chimodzi. Zina zonse zidzayenera kuti zidzathe. Izo zinali zopotozedwa kuchokera ku kasupe weniweni uyu.

259 Tsono, chotero, gehena, kuzunzika, kuzunzika si Kwamuyaya. Kuzunzika kunabweretsedwapo chifukwa cha tchimo, ndipo tchimo linayambitsa kuzunzika. Ndipo pamene tchimo lidzathetsedwa, kuzunzika kudzayenera kuti kudzathe, nakonso. Ndipo idzakhalapo nthawi pamene ochimwa, omwe sanamulandire konse Khristu, iwo atatha kulangidwa mwinamwake kwa zaka mabilioni zana, ... Ine sindikudziwa, mwinamwake kwa zaka mabilioni milioni makumi zana. Ine sindingakhoze kunena. Koma izo zidzayenera kudzafika pa mathero, nthawiyina, chifukwa izo si Zamuyaya.

260 Tsopano, ife tikuti tilimbikire mopitirira tsopano, kumka cha ku ngwiro. Tsopano mvetserani, pamene ife tikulowa mu Uthengawu.

...osati kuikanso maziko a kulapa kuchokera ku ntchito zakufa, ndi kuchokera ku chikhulupiriro cha kwa Mulungu,

Za chiphunzitso cha maubatizo, . . . kuikapo kwa manja, . . . chiukitsiro cha akufa, ndi . . . chiweruzo chamuyaya.

²⁶¹ Tsopano tamvetserani. Ife tiri nazo ziwiri. Ife tiri ndi chithunzi apa, tsopano. Tsopano apa pomwe ndi pamene ife titi tipeze kusagwirizana kwina kwakukulu. Tsopano inu muyenera kuwona pomwe chithunzicho chiri. Paulo akuyesera, apa, kuti alekanitse *lamulo* kwa *chisomo*. Ife tiri ndi zithunzi ziwiri: chimodzi, chachithupi; china, chazimu. Ndipo Paulo akuyesera k—kuti apatuke pakati pa ziwirizo, kuti awasonyeze Ayuda. Kalata iyi ndi ya kwa Ahebri. Ndipo Ahebri onse akuyesera kuti awasonyeze ndondomeko ya Chipangano Chakale chikuimira Chatsopano. Chotero, inu muli nazo zithunzi ziwiri apa zoti muzilingalire.

²⁶² Tsopano mvetserani mwatcheru pamene ife tikuwerenga. Tsopano iye anati:

. . . kusiyana nazo zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipite mpaka ku ungiro; . . .

²⁶³ Tsopano, ife tinali nazo izo mmawa uno, momwe ife timakhalitsidwira angwiro. Kupangidwa angwiro, mwamtheradi opanda banga ndi opanda chilema, opanda tchimo limodzi pa ife. Kodi inu muli pamwamba pa yesero? Ayi. Kodi inu mumachimwa tsiku lililonse? Inde, bwana. Koma, komabe, ife timakhalitsidwa angwiro chifukwa ife tiri mwa Iye. Ndipo Mulungu sangakhozenso kutiweruza ife kuposa kalikonse (sangati akhale wolungama), Iye anatiweruza kale ife mwa Iye. Pamene Iye anamuweruza Khristu: Iye anandiweruza ine, Iye anakuweruzani inu. Ndipo Iye sangati andiweruze ine kachiwiri, chifukwa Iye anatenga chiweruzo Changa ngati ine ndinawomboledwa kale.

²⁶⁴ Ndipo ine ndiri nacho chiphaso chosonyeza kuti ine ndawombola wochi yanga kuchokera ku sitolo ya zopinyolitsa, winawake ayelekeze kuti aitenge iyo kubwereranso mu shopu ya zopinyolitsa nthawiina, pamene ine ndiri ndi chiphaso. Ine ndaiwombola iyo kale.

Ndipo ngati Mdierekezi angayesere kuti ayike chilango pa ine, ine ndiri ndi chiphaso chomwe chikusonyeza kuti ine ndinawomboledwa kale. Inde, bwana. Palibe chiweruzo china! “Iye amene amva Mawu anga, ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Icho ndi chiphaso changa. Iye anapereka lonjezo.

²⁶⁵ Tsopano, tsopano chithunzichi, apa.

. . . osati kuikanso maziko a kulapa kuchokera ku ntchito zakufa, ndi . . . chikhulupiriro cha kwa Mulungu,

*... chiphunzitso cha ubatizo, ... kuika kwa manja, ...
chiukitsiro cha akufa, ... chiweruzo chamuyaya.*

266 Tsopano, kumbukirani, inu mukuzindikira mawu awo akugwiritsidwa ntchito kachiwiri? Ife tinawagwiritsa iwo ntchito mmawa uno, “chiweruzo Chamuyaya.” Pamene Mulungu ayankhula kamodzi, Izo ndi Zamuyaya. Izo sizingakhoze kusinthidwa, npang’ono. Chotero, chiweruzo ndi Chamuyaya, Icho nthawizonse chiri chiweruzo. Ndipo ziribe kanthu kam’badwo komwe ife tikukhalamo, kam’badwo kamodzi kadzakhala moyo, ndi kamodzi . . . tonse tidzakhala moyo, ndipo ndi za kwanthawizonse, kwa nthawi ina iliyonse, ndi *izi* ndi *izo*. Koma chiweruzo cha Mulungu chikadali Chamuyaya, Iye ayenera kutero, chifukwa Iye anayankhula Mawuwo. Pamene Mulungu ayankhula Mawu, Iwo amayenera kukhala Amuyaya. Ndiko kulondola.

267 Tsopano ndiroleni ine ndiwerenge izo kuchokera mu Chigriki kwa inu. Mvetserani momwe izo zikuwerengekera.

*Chotero posiya—posiya zoyambirira za ziphunzitso
za Khristu, wotetezedwa Uyo, ife tiyenera tikankhe—
tikankhire cha ku . . .*

Tsopano, ine sindikukhoza kuziwerenga izo. Izo zaziralirapo. “Ndipo osati kuikanso mawonekedwe . . .” Apa ife tiri.

*. . . osati kuikanso mawonekedwe a kukonzanso
kuchokera ku ntchito zoyambitsa imfa.*

268 Tsopano, lexiconi iyi ili mwamtheradi yopanda kutanthauzira kulikonse, nkomwe. Ndi mawu Achigriki basi a chomwe Chingerezi chikunena. Ndipo iwo anati, “Tsopano ife sitikufuna . . .” Mvetserani apa, onani.

*. . . osati kuika apo maziko a kukonzanso kuchokera
ku ntchito zoyambitsa imfa.*

269 Tsopano ngati inu mungazitengere izo mu malingaliro anu, zomwe iye akuyankhula apa, kuti, “Zimango za kukonzanso zimayambitsa imfa.” Paulo anati, “Posiya zoyambirira, tipite ku ungwiro, osati kuikanso maziko a kulapa kuchokera ku ntchito zakufa ndi chikhulupiriro cha kwa Mulungu: ziphunzitso za ubatizo, kuyikapo kwa dzanja, chiukitsiro cha akufa, chiweruzo Chamuyaya. Machitidwe akukonzanso woyambitsa imfa,” anali mawu olondola. Ndizo makamaka zomwe Paulo analemba. Mukuona zomwe iye akuyesera kuchita?

270 Tsopano, zinthu zonse izi, monga maubatizo: wina amabatizidwa chammbuyo, wina chamtsogolo, wina mu dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera, wina dzina la Yesu, wina njira *iyi*, ndi njira *iyoyi*, ndi zinthu zonse zazing’ono zosiyana izi za maubatizo.

271 Ndi za kuikapo kwa manja: “Mulungu adalitsidwe, ine ndiri nayo mphatso ya kuikapo kwa manja. Aleluya! Inu, inu mukhoza kuipeza Iyo mwanjira *iyi*. Aleluya!”

272 Kuyika zonse izo pambali, chifukwa izo ndi ntchito zakufa, kukonzanso uku, kukonzanso. Mukuona? Iye akuyankhula za gulu lina. Tsopano iye anati, “Tiyeni tichoke kwa izo, ndipo tipitirire mpaka ku ungwiro.” Inu mukumvetsa Izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

273 Ndipo mpingo ukadachedwa mmbuyo mu zinthu zimenezo. Ndi zomwe iwo ankayesera kumazichita. Mpingo woyambirira wa Chihebri unkayesera kunena kuti, “Chabwino, ine ndinabatizidwa mwa kumiza, n—ndipo ine ndinapeza *izi*, ndi *izi*, ndi zinthu zonse *izi*.”

274 Iye anati, “Tsopano, ikani zonse izo kumbali, kuzisiya izo mmbuyo.” Koma, tsopano, kodi iye anati ife tisamachite izo? Tsopano mvetserani kwa zomwe iye ananena pa izo.

Ndipo izi ife tizichita, . . . Mulungu akalola.

275 Ndipo mwapachiyambi ilo linanena chinthu chofanana.

Izi ife tizichita, ngati Mulungu atilola ife, mwaona.

Izi ife tizichita, ngati Mulungu atilola ife.

276 Maubatizo, kuikapo kwa manja, ndi zinthu, koma izo si zangwiro. Uko ndi kukonzanso chabe kwachithupithupi. Ndipo ndi pamene mipingo imalekezerapo, lero, ndi pa kukonzanso kwa chithupithupi uko. Mmodzi wa iwo anati, “O, chabwino, madzi, mawu oti *ubatizo* amatanthauza *ichi* ndipo iwo amatanthauza *icho*.”

277 Ndipo iwo anakhazikitsa mabungwe: ndipo wina amakonkha, winayo amatsanulira, winayo amabatiza chafufumimba, winayo chagada, ndi zinthu zonse izo; ena a iwo kuikapo manja pa odwala, ndipo ena kupanga atumwi, ndi ena kupanga aneneri ndi zina zotero, mwa kuikapo kwa manja; ndi kulalikira za chiukitsiro kuchokera kwa akufa, ndi zomwe ziri zabwino; ndi Umulungu wapamwamba wa Khristu, izo zonse nzabwino. “Koma,” iye anati, “zonse izi ndi kukonzanso kwachizolowezi. Ife tiri kungokonzedwanso. Tsopano tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro.” Inu mukuchigwira chithunzicho? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

278 Tsopano penyani. Apa ndi pamene gawo lakuya likubwerapo tsopano.

Pakuti ndi kosatheka kwa iwo omwe anayamba awunikiridwapo, ndipo analawa za mphatso yakumwamba, ndipo anapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera,

Ndipo analawa za mawu abwino a Mulungu, . . . mphamvu ya dziko likudza,

Ngati iwo angati agwe, kuti awakonze iwo kachiwiri ku kulapa; powona kuti iwo akudzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu kachiwiri, ndi kumuika iye mu manyazi apoyera.

279 Tsopano, ine ndikudziwa zomwe inu azamalamulo muli nazo mu malingaliro anu pakali pano, koma inu mukulakwitsa. Mukuona? Chabwino. Ine ndikuima pa ichi, ndipo Baibulo likutsimikizira icho, kuti, “Ngati Mulungu amupulumutsa konse munthu, iye amapulumutsidwa kwa nthawi ndi kwa Muyaya.” Inu simungazipange Izo kunena china chakenso.

280 Wachikhazikitso wina anabwera kwa ine, si kale litali, ndipo anati, “Inu ndakugwirani inu pa chimodzi, Mlaliki Branham. Ine ndakugwirani inu chimodzi. Inu munati, ‘Ngati munthu apulumutsidwa, iye sangakhoze konse kutaika?’”

281 Ine ndinati, “Izo ndi zomwe Mulungu ananena.”

282 Iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Sauli anali mneneri, ndipo iye ankanenera. Ndipo inu mukudziwa kuti iye anali wodzozedwa wa Mulungu. Baibulo linati iye anali. Ndipo iye anadziza, ndipo iye anataika.”

283 Ine ndinati, “Iye anali? Ine ndinati, “Baibulo limanena kuti iye ‘anapulumsidwa.’ Iye atakhala mdani kwa Mulungu, iye anali wopulumutsidwabe. Baibulo linati iye anali. Ndipo, pambuyo pa zonse, iye sanachite kudzipha. Mfilisti anamupha iye, ndipo Davide anamupha Mfilistiyo chifukwa chomupha iye. Iye anagwera pa lupanga lake, mpaliro wake, lupanga, koma, iye anatero. Ilo silinamuphe iye. Ndi Mfilisti anamupha iye. Ndiyeno pamene Sauli anapita kuja kwa msing’anga, ndipo iyeyo anaitanitsa mzimu wa Samuele, chifukwa iye anali asanalowe ku Ulemerero, iye anali mu paradiso pansa pa magazi okhetsedwa a ng’ombe ndi mbuzi omwe sankakhoza kulichotsapo tchimo. Koma iye ankayenera kukhala ndi malo odikirirako, omwe amatchedwa paradiso, mpaka iye atadzalowa umo.”

284 Ndi pamene inu anthu Achikatolika munasokonezeka. Mukuona? Tsopano, palibe paradiso winanso tsopano. Iye timapita molunjika mu Kukhalapo kwa Mulungu.

285 Ndipo pamene msing’anga waku Endori anawuitana mzimu wa Samuele, apo iye anaima. Ndipo iye anagwa chafufumimba, ndipo iye anati, “Chifukwa chiani inu mwandinyenga ine?”

286 Ndipo sikuti Sauli anaima kokha apo. . . Ine ndikutanthauza Samuele, mu mwinjiro wake wa mneneri, iye anali akadali mneneri. Iye anati, “Nchifukwa chiani iwe wandiitana ine kuchokera mu kupumula kwanga,” anati, “powona kuti iwe wakhala mdani kwa Mulungu?”

287 Iye anati, “Pakuti, Urimu sakuyankhula kwa ine panonso. Mneneri sakukhoza kulosera kwa ine panonso. Ngakhalenso ine sindikukhoza kukhala ndi loto.”

288 “Chabwino,” Samuele anati, “iwe wasanduka mdani kwa Mulungu. Koma mawa nkondo ipita kumbali ina, ndipo iwe ufa mawa. Ndipo pofika nthawi ino, mawa usiku, iwe udzakhala uli ndi ine.” Ngati Saulo anali atataika, chomwechonsotu Samuele, iwo anali onse limodzi. Ndithudi. Baibulo linanena chomwecho.

289 Tsopano, inu mukhoza kukhala yense wodzipangitsa mu kutengeka, pakuyankhula mu malirime, kufuula, kugwedezeke, kuthamanga chokwera-ndi-chotsika mu kanjira. Ndiribe zotsutsa izo. Koma iwe ukhoza kudzipanga wekha kukhulupirira kuti iwe unapulumutsidwa pamene iwe usali, iwe suli wopulumutsidwa. Moyo wako umatsimikizira chomwe iwe uli. Yesu anati iwo ukanatero, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Moyo wanu umatsimikizira ngati inu munapulumutsidwa kapena ayi, ngati inu simutsegula konse kamwa yanu. Iwo umatsimikizira chomwe inu muli.

290 Koma zodzipangitsa zonse izi ndi zotengeka ndi kujowina mpingo, “Ndipo ine ndinabatizidwa mu Dzina la Yesu, aleluya, ine ndikudziwa ine ndiri nawo Iwo,” izo sizimatanthauza kanthu.

291 “Ine ndinabatizidwa, mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera, chafufumimba, katatu. Ine ndiri nawo Iwo.” Izo sizikutanthauza kanthu.

292 Paulo anati, “Tiyeni tipitirire mpaka ku ungwiro tsopano.” Ife tikuyankhula za kupangidwa kukhala wangwiro. Ndipo ngati ife titayendetsa izi motsika, inu mungapeze kuti, angwiro ndi Osankhidwa. Ine nditsimikizira izo kwa inu, mu maminiti pang’ono, mwa Baibulo. Ndi Osankhidwa omwe Mulungu, asanaikidwe maziko a dziko, anawaona aliyense wa iwo. Ndipo Iye anamutuma Yesu kuti adzawaombole anthu amenewo, osati dziko lonse. Iye ankafuna kutero, koma Iye anayenera kupanga njira kwa amenewo. Ndipo njira yokha yomwe Iye akanakhoza kuchitira, inali kumutumiza Khristu; kuti Iye akhoze kubwera, chitetezero cha machimo athu, kuti iwo omwe anali atasankhidwa, Iye akanakhoza kuwabweretsa kwa Iye, mu Ulemerero.

293 Kodi inu mukanakhoza kulingalira Mulungu kuyendetsa ntchito Yake mosasamala chotero, ngati kuti, “Chabwino, mwinamwake winawake aganiza mwachisoni kwenikweni za Ine, mwinamwake iwo abwera ndi kudzapulumutsidwa”? Mulungu samasowa kuti akupempheni inu kuti muchite chinachake ayi. Kupempha kulikonse, inu mukusowa kuti muzichita kupemphako, osati Mulungu.

294 Ndiyeno, Khristu anafa kuti awapulumutse iwo omwe Mulungu, mwakudziwidwiratu, anawasankha kuti adzakomane naye Iye kutsidyako opanda banga kapena khwinya. Asanaikidwe maziko a dziko, Iye anakuwonani inu mu Ulemerero. Ndicho chimene Baibulo linanena, Aefeso, mutu

wa 1. Mutu wa 5, ndime ya 1. Mulungu anakonzeratu mwa kudziwiratu.

²⁹⁵ Tsopano, ngati Mulungu anachita zimenezo, anatikonzeratu ife asanaikidwe maziko a dziko; ndipo anamudziwa aliyense wa ife ndi dzina, asanaikidwe maziko a dziko; ndipo Iye anatisankhira ife ku Moyo Wamuyaya; ndipo anamutuma Yesu Khristu kuti adzatiwombole ife; kuti, zaka mazana asanu ndi amodzi zapitazo, Iye anatiwona ife, kuti ife tikakhoze kuwonekera kwa matamando Ake mu Ulemerero! Inu mungakhoze konse kutaika chotani?

²⁹⁶ Tsopano, ngati inu munapululumutsidwa, inu munapululumutsidwa. Ngati Mulungu angakupulumutseni inu usikuuno, akudziwa kuti Iye adzakutayani inu zaka khumi kuchokera lero, Iye akugonjetsa cholinga Chake chomwe; Mulungu wopandamalire, Wamphamvuzonse, Wamuyaya, wanzeru zosatha, samadziwa mokwanira ndiye kuti adziwe ngati inu muti mudzagwirebe kapena ngati inu simudzatero. Ndiye, pamene Iye akupulumutsani inu, inu mukuti, “Chabwino, ine ndimupatsa Iye yesero. Ine ndiwone zomwe Iye ati achite,” ndiye Iye samadziwa mapeto kuchokera kuchiyambi. Mulungu amadziwa zomwe Iye akuchita, inu musati muzidandaula konse za izo. Ndi inuyo ndi ine tikupunthwa mu njirayi. Mulungu akudziwa zomwe Iye akuchita. Ndipo Iye anatidziwa ife. . . kaya ife tikanagwirabe, kapena zomwe ife tikanati tichite.

²⁹⁷ Tsopano, Baibulo linanena kuti, Esau ndi Yakobo, mwana aliyenseyo asanabadwe, Mulungu anati, “Ine ndamukonda mmodzi, ndipo ndamuda mmodzi winayo,” iwo asanapume ngakhale mpweya wawo woyamba, kuti kusankha Kwake kukhoze kumaima koon.

²⁹⁸ Kodi Abrahamu anali ndani? Ife tifika kwa iye mu maminiti pang’ono, pamusi apa. Iye anali ndani, kuti Mulungu amuitane? Anamupulumutsa iye popanda chirichonse. Mulungu amapanga pangano ndi munthu; munthu amaswa pangano lake. Koma Mulungu anapanga Pangano ili ndi Iyemwini, ndipo analumbira pa izo, kwa Iyemwini. Munthu alibe kanthu kochita nazo. Ndi kudziwidwiratu komwe kwa Mulungu. Iye anachita izo, basibe.

²⁹⁹ Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, ndiye ngati ine ndikanakhala Mkhristu, ine ndikanakhoza kumangochita chirichonse chomwe ine ndikanafuna kuchichita?” Mwamtheradi. Ngati iwe uli Mkhristu, zichita chirichonse chomwe iwe ukufuna kuchichita. Ndipo ine ndikulonjeza, iwe sukhalala ndi chikhumbo chirichonse kuti ukachite cholakwika. Iwe zichita chirichonse. Ine nthawizonse ndakhala ndikuchita basi zomwe ine ndimafuna kuzichita. Ndipo ngati ine ndikumutumikira Ambuye chifukwa choti ine ndikuwopa kuti ine ndipita ku gehena, ine sindikumutumikira Iye moyenera. Ngati ine ndikukhalala mooni kwa mkazi wanga

chifukwa ine ndikuwopa kuti iye andisudzula ine, ine sindiri mwamuna wabwino kwambiri. Koma ine sindikanamupweteka iye pa kena kalikonse, pakuti ine ndimamukonda iye.

³⁰⁰ Umo ndi momwe ziriri ndi Khristu, pamene munthu abadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Osati chifukwa iye anafuula, anayankhula mu malirime, kapena kutengeka kwinakwake; koma mu mtima mwake, chikondi chinabwera umo ndipo chinatenga malo a zadziko. Ine ndikukuuzani inu, iye amamukonda Iye. Iye amayenda pafupi ndi Iye, tsiku lililonse. Inu simusowa kuti muzichita kumuza iye, “Ndi kulakwa kuchita izi, kapena *izo*, kapena *zinazo*.” Iye amadziwa kuti ndi zolakwika. Ndipo, iye amayenda, iye ndi chinthu chodzozedwa cha chisomo chamwayekha cha Mulungu. Ndendende.

Pakuti ndi kosatheka kwa iwo omwe nthawi ina anawunikiridwapo, . . . napangidwa kukhala ochita nawo a . . . kuitana kwakumwamba . . .

Tsopano, ife nthawizina takhulupirirapo kuti uyo anali munthu yemwe nthawiina anawunikiridwapo ndipo anagwera kwina kachiwiri, koma Baibulo silimawerengetsa izo mwanjira imeneyo. “Ndi zosatheka mwamtheradi kwa munthu,” iye akutero apa, “yemwe analandira Mzimu Woyera, kuti adzagwere kwina konse.” Tsopano werengani izo ndi kupeza ngati izo si zolondola. Penyani apa, tengani nkhaniyo, nkhani yonse, ndi zirimozo, phunzirolo, kani.

³⁰¹ Tsopano Iye akuyamba kuyankhula, ndi chiani icho? “Tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro.” Tsopano, iye anati, “Osati zachithupithupi, kuika maziko apa a tiziphunzitso ndi ubatizo ndi kukonzanso, ndi zina zotero. Tiyeni tisamachite izo. Tiyeni tipitirire mpaka ku ungwiro.” Phunziro ndilo *ungwiro*, ndipo ungwiro umadza ndi Khristu. Ndipo kodi ife tinalowamo chotani mwa Khristu? Pa kujowina mpingo? “Ndi Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi.” Osati mwa: kuyankhula kwa lirime, kumodzi; kugwirana chanza, kumodzi; ubatizo wa mmadzi, umodzi. “Koma mwa Mzimu umodzi ife timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi.” Inu mukuzimvetsa izi? Uwo ndiwo ungwiro.

³⁰² Ndipo pamene inu mubwera Mmenemo, inu muli mwa Khristu, ndipo dziko liri lakufa kwa inu. Ndipo inu mukuyenda ndi Mwanawankhosa tsiku lililonse, ndipo masitepe anu ali odzozedwera Mulungu, choti nkuchita. O, mayesero ndi zoyesa zomwe ife timadutsamo! Inu mukuti, “Kodi inu mumakhala ndi kuyesedwa?” Inde, bwana. Chomwe chiri . . .

³⁰³ Chisomo ndi chomwe Mulungu anandichitira ine, ntchito ndi zomwe ine ndimamuchitira Mulungu. Tsopano, iwo apanga chiphunzitso kuchokera pamenepo, iwo akuganiza kuti ntchito ndi zomwe zimapangitsa kuyenera kwako. Ngati izo ziri, iyo si mphatso yaulere. Chisomo ndi chimene Mulungu anakuchitirani

inu, “Mwa chisomo inu munapulumsidwa.” Ndipo ntchito ndi zomwe inu mumachita poyamikira chisomo chomwe Iye anasonyeza kwa inu. Ndipo ngati inu mukumukonda Iye, inu muzikonda kumachita ntchito za Ambuye. Ndithudi, chifukwa, ndiye, i—inu mukumukonda Iye.

³⁰⁴ Kumuvomereza Meda Broy, ngati mkazi wanga, chinali chomwe chikondi chinamuchitira iye. Zomwe iye achita, mwa kuyamikira: iye ndi mkazi wabwino, amakhala pakhomo, amawasamalira ana, ndipo amakhala moyo wabwino wona. Izo sichifukwa chakuti ife sitinakwatirane; ife tinakwatirana. Koma iye amachita zimenezo mwa kuyamikira. Ngati iye azithamangira mu mzinda, tsiku lililonse, ndi kukalowa mu sitolo ya teni senti iliyonse, ndi chokwera ndi chotsika mmisewu, ndi kusamatsuka konse mbale, kapena china chirichonse, ife tikanali okwatiranabe. Mwamtheradi. Pamene ine ndinatenga lumbiro langa, izo zinakhazikitsa icho. Iye ndi mkazi wanga. Utali wonse pomwe muli moyo mwa ife, iye ndi mkazi wanga. Ilo linali lumbiro lake. Koma kuyamikira komwe iye amapanga pa izo: iye amakhala kunyumba, ndipo amawasamalira ana, ndi kuyesera kuti azikhala mkazi weniweni.

³⁰⁵ Ine ndikhoza kumathamangira kunja ndi kukhala nditachokapo nthawi zonse, kumangokayenda ku midzi, ndi kumusiya iye pafupi kufa ndi njala, kapena chirichonse, kuwasiya ana kumakayenda opanda kanthu kotu adye; ife tikanali okwatiranabe. Ngati iye ngakhale atandisudzula ine, ine ndikanali wokwatira, bola ngati muli moyo mu thupi langa. Ine ndinatenga lumbiro limenelo, “Mpaka imfa tidzalekana.” Ndiko kulondola. Ife tiri okwatiranabe. Koma, apabe, ine ndikupanga kuwiringula kosauka kwa mwamuna. Iye angamapange kuwiringula kosauka kwa mkazi. Chotero ngati ife tikukondana wina ndi mzake, ife timamamatirana limodzi ndi kukoka katunduyo palimodzi.

³⁰⁶ Umo ndi momwe Mulungu ndi Mpingo Wake aliri, pamene iwe ubadwira mu Ufumu wa Mulungu. Iwe umakhala nazo *zitunda* ndi *zitsika* zako, zooni, koma iwe ukadali Mkristu, iwe ukanali wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu. Mulungu akhoza kukuchotsa iwe padziko lapansi mofulumirirapo.

. . . ndi *kosatheka kwa iwo* omwe *anawunikiridwapo kamodzi*, *ndipo analawa* . . . *mphatso ya kumwamba*, . . .

. . . kuti *adzagwe* konse, *kuti adzibwezerenso* iwoeni *kachiwiri ku kulapa*; . . .

³⁰⁷ Tsopano, ine ndikudziwa pamene inu mukupaganizirapo, mpingo. Ndiroleni ine ndingokutengerani inu chimodzi champhamvuko pang’ono, chotero—ambali ya zamalamulo akhoza kutonthola kwenikweni. Tiyeni ife tipite ku Ahebri, mutu wa 10, ndi kukayang’ana pa ichi kwa pang’ono pokha.

³⁰⁸ Mutu wa 10, ndime ya 26.

Pakuti ngati ife tichimwa mwadala titatha...ife kulandira chidziwitso cha choonadi, sipamakhalanso nsembe ina ya kwa tchimolo,

Koma kuwonekera kwina kowopsya...kwa chiweruzo ndi mkwiyo woyaka, womwe uti udzamuwononge mdani.

Iye yemwe ankanyozetsa lamulo la Mose ankafa mopanda chifundo pansi pa mboni ziwiri kapena zitatu:

Ndi chilango chowawa mochuluka bwanji, ngakhale akuchilingalira...ngakhale kuyenera,... anaponda... omwe anapondereza pansi pa phazi Mwana wa Mulungu, ndi kuwawerengera magazi a pangano, omwe iye anayeretsedwa nawo, ngati chinthu chosayera, ndipo... achita monyalanyaza ku ntchito za chisomo?

³⁰⁹ Tsopano inu mukuti, “Nanga bwanji zimenezo, M’bale Branham? Izo zikuwoneka motani?”

Tsopano, kungoti tiwerenge, ine ndikuganiza, “Lemba silikunena zimenezo.” Izo sikuyankhula za Mkristu. Izo zikuyankhula za munthu yemwe anamva Mawu ndipo anapotoloka nachoka kwa Iwo. Mukuona?

Pakuti ngati ife tichimwa... (Kodi tchimo ndi chiani? Kusakhulupirira)... ngati ife tichita kusakhulupirira mwadala uthenga utalalikidwa kale kwa ife, apo sipamakhalanso nsembe ina ya kwa tchimolo,

³¹⁰ Kodi tchimo ndi chiani? Kusakhulupirira. Kawerengeni Yohane Woyera, mutu wa 4. Yesu anati, “Iye amene sakhulupirira waweruzidwa kale.” Tchimo si kusuta, kumwa, kuchita chigololo. Iwe umachita zimenezo chifukwa ndiwe wosakhulupirira. Izo ndi zotsatira chabe. Iwe umachita zimenezo chifukwa ndiwe wosakhulupirira. Kungosiya kusuta, kusiya kumwa, ndi zina zotero monga izo, izo sizimatanthauza kuti iwe—ndiwe Mkristu. Izo ndi zotsatira chabe za kutembenuka kwako. Koma, iwe ukhoza, iwe ukhoza kuchita mbali iliyonseyo, ndi kusakhalabe uli.

³¹¹ Tsopano zindikirani.

... iye amene sakhulupirira *mwadala atatha* iye...

³¹² Osati—osati, “Iye atamulandira kale Khristu mu mtima mwake.” Baibulo silimanena zimenezo. Anati, “Iye yemwe...”

...ngati ife tichimwa mwadala, kusakhulupirira mwadala, titatha...ife kulandira chidziwitso cha choonadi,...

Mwamvetsa izo? Sanali kuyankhula kwa Mkristu, konse.

313 Mkazi wina anabwera kwa ine, si kale litali, ndipo anati, “M’bale Branham, ndine Mkhristu, koma ine ndachitira mwano Mzimu Woyera.”

314 Ine ndinati, “Ndi zosatheka.” Mkhristu sangakhoze kuchitira mwano Mzimu Woyera. Inu simungakhoze kuchita izo. Mzimu wa Mkhristu umachitirana umboni ndi Mzimu wa Mkhristu. Mukuona? Ndipo inu mumachitcha, chirichonse cha Mulungu, “cha Mulungu.”

315 Koma ngati inu muli amalingaliro achithupithupi, inu muziuseleula ndi kuwuseka Mzimu Woyera; ine sindikusamala kuchuluka kwa momwe inu mumapitira ku mpingo, inu mukadali wochimwa, ndipo inu mukuchitira mwano Mzimu Woyera. Pamene iwo anamuwona Yesu akuzindikira malingaliro awo, iwo anati Iye anali “wambwebwe.”

316 Yesu anati, “Inu . . . ine ndikukhulukirani inu pa izo, koma pamene Mzimu Woyera udzadza, inu mukadzayankhula mawu motsutsa Iwo, izo sizidzakhulukidwira konse kwa inu.”

Chifukwa, iwo anati, “Iye ali ndi mzimu wosayera,” kuwutcha Mzimu wa Mulungu, “chinthu chosayera.” Mkhristu sangakhoze kuchita zimenezo. Mkhristu nthawizonse aziwutcha Mzimu wa Mulungu, “Chilungamo.” Mukuona? Mkhristu sangakhoze kuchitira mwano Mzimu Woyera. Ndi wakunja yemwe amachitira mwano.

317 Ajawa sanali Akhristu ataima pamenepo. Iwo anali anthu achipembedzo, iwo anali Ayuda achiorthodox, modotolo azauzimu, ndi zina zotero, ndipo iwo anali akumunyogodola Iye ndi ntchito Zake, kumazitcha ntchito za Mulungu, kuti, “Izo zinali mzimu wosayera umachita izo.”

318 Ndipo ndi angati omwe inu mukuganiza lero kuti akuchitira mwano Mzimu Woyera, omwe ali ndi D.D.D., PhD. pa dzina lawo? Ndi aakulu angati, Achiorthodox okhuthala, Achikatolika, Achiprotestanti, amayenda mu msewu ndi kumanyogodola kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera, masikolala basi opukutidwa, ndi owala ngati batani? Uko nkulondola. Koma iwo amawunyogodola Mzimu Woyera, ndipo chotero iwo amachitira mwano Iwo.

Koma Mkhristu wobadwa-kachiwiri sangakhoze kuchita zimenezo. Iye angati, “Uyo ndi m’bale wanga. Uwo ndi Mzimu wa Mulungu wamoyo.” Ndiko kulondola. Mkhristu sangakhoze kuchitira mwano Mzimu Woyera.

319 Ndi wochimwa yemwe amachitira mwano Mzimu Woyera; wosakhulupirira, *wochimwa*, “wosakhulupirira.” Pali zinthu ziwiri zokha: mwina ndiwe wokhulupirira, kapena wosakhulupirira.

320 Tsopano, zindikirani apa, kuti tizipangitse izi kumangirizana kwenikweni tsopano. Ine ndinali ndi

masomphenya omwe akhala akundivutitsa ine nthawizonse. Zaka zapitazo ine ndinkakonda kuyang'ana pa izo. Ine ndinkati, "O, ngati munthu anayamba walandirapo Mzimu woyera, ndiyeno iye nkubwerera mmbuyo, iye akanati adzataike kwa nthawizonse." Ine sindinkakhoza kupeza china ichi kuti chipangitse kumveka ndi icho.

³²¹ Ine ndinati, "Ndiye bwanji ziri kuti Baibulo linanena, kuti, 'Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine ali nawo Moyo Wamuyaya, Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Onse omwe Atate anandipatsa Ine adzadza kwa Ine, ndipo palibe mmodzi wa iwo adzataike, Ine ndidzawautsa iwo mu masiku otsiriza. Palibe munthu angawakhwathule iwo kuchokera mdzanja Langa'? Kodi zimenezo zikugwirizana bwanji ndi izi? Ine sindinkakhoza basi kuzimvetsa izo, 'Ndi kosatheka kwa iwo omwe nthawiyina anaunikiridwa.'" Ine ndimaganiza, "Pali chinachake cholakwika. Ine sindikukhoza basi kuzimvetsa izo."

Ndipo ine ndinapita ku msonkhano wawung'ono wa Achipentekoste, zaka zapitazo.

³²² Palibe mmodzi yemwe watsalira mu mpingo, ine ndikuganiza, usikuuno, yemwe akuzikumbukira zimenezo. Zaka zapitazo, iyi inali ngakhale pafupi basi nthawi yomwe kachisi yu ankamangidwa. Kupatula, angakhale M'bale Graham kumbuyo uko, kapena winawake. Ine sindikudziwa, inu munali woyamba kufika kuno, kapena ayi, abale. M'bale Mahoney, ine ndikuganiza, anali. Eya, ine ndisanakwatire basi.

³²³ Mphatso ija ikugwira ntchito, ine ndinkachita mantha. Iwo ankandiuza ine kuti izo zinali za Mdierekezi. Ine sindinkadziwa mpaka Mngelo wa Ambuye atadzandiuza ine.

³²⁴ Ine ndinapita ku Mishawaka, ndipo ine ndinali mu msonkhano umenewo, ndipo ine ndinali ndisanayambe ndamvapo kufuula kochuluka chotero ndi kulira ndi kumutamanda Mulungu. Ine ndinaganiza, "M'bale, kuno ndi Kumwamba." Ndipo, o, momwe iwo amakwerera ndi kutsikira.

³²⁵ Iwo anayenera kukauchitira iwo Kumpoto, pa chifukwa cha tsankho. Achikuda ndi azungu anasonkhana palimodzi. P.A. wa W. ndi P.H.A.C. anali atalumikizana kwenikweni ndipo anakhala United Pentecostal. Koma chitsitsimutso chake chomwe iwo anali kukhala nacho, uko ku kachisi ya M'bale Rowe ku Mishawaka. Ndipo ine, kamunthu kakang'ono kofunitsitsa kudziwa, nditakhala pa mpando wakumbuyo, ndinali kuziyang'ana zonse izi. Ine ndinali ndisanawonopo zinthu izi kale.

³²⁶ Apo panali bambo atakhala apa...Ine sindinayambe ndanenapo izi pagulu kale. Panali bambo atakhala ku mbali imodzi, ndi bambo kumbali inayo, ndipo mmodzi

ankayankhula mu malirime, ndipo winayo ankanthanzira izo. Ndipo iwo ankakhoza kunena zinthu zosiyanasiyana zomwe zikanati zichitike. Ndiye, *uyu* ankayankhula mmalirime, ndipo *winayo* ankanthanzira. Ine ndinaganiza, “Mai, kodi izo sizodabwitsa!” Ine ndinaganiza, “Ulemerero wakewo! Awo ayenera kukhala ali Angelo, atabwera pansu mwa mawonekedwe a anthu.”

³²⁷ Chabwino, ine ndinali ndi dola ndi masenti sate-faifi zokha, zoti ndibwerere nazo kwathu, ndipo i—i—ine ndikanangokhoza kupeza thanki ya mafuta. Ine ndinagona mmunda wa chimanga usiku umenewo. Ine ndiri nazo gawo la izo mu bukhu, koma osati zonse za izo, chifukwa ine sindinkafuna kuti ndipweteketse kumverera kwawo. Ndipo chotero, usiku umenewo, iwo anati, “Alaliki onse abwere pa nsanja.” Ine ndinali pa nsanja. Ine ndinali mlaliki wamng’ono kwambiri apo ndiye.

³²⁸ Chotero, mmawa wotsatira, iwo anandifunsa ine kuti ndibwere ndidzalalikire. Ine ndinabisala. Inu mukudziwa, bambo wachikuda anati, “Uyu ali apayu.” Inu mukukumbukira nkhanu ya izo, pamene iye anandiwulula ine nditakhala pamenepe.

³²⁹ Ndipo kotero nditatha kulalikira tsiku limenelo, ndikuyenda yenda, ine ndinaganiza “Ngati ine ndikanakhoza kokha kufika kwa amuna awiri aja.” Iwo amatsogolera msonkhano. Wina amauka ndi kukhala woyera pa nkhope; iye amakhoza kuyankhula mmalirime. Ndipo winayo amakhoza kutanthanzira izo, ndi kupereka mawu, “PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Pali munthu *wakuti-wakuti* pano, dzina lake *wakuti-wakuti*, yemwe ayenera kuti achite *izi* ndi *zakuti-zakuti*.” M’bale, izo zinali zoono. Ndipo winayo amakhoza kuwuka ndi kuyankhula mmalirime, ndipo iyeyu amakhoza kutanthanzira.

³³⁰ Ine ndinaganiza, “O, mai, kodi izi sizodabwitsa!” Chotero, tsiku limenelo, ine ndinaganiza, ine ndinapita kwina ndi kukapemphera. Ine ndinaganiza, “Ambuye, inu mundichitire zijazi ine panonso.” Ine sindinkadziwa choti ndizizitcha izo, masomphenya.

³³¹ Ine ndinapita kwina ndipo ndinakupemphera, ndipo ndinawafunsa Ambuye kuti andithandize ine. Ine ndinapita mozungulira nyumba, ndipo ine ndinapezeka kuti ndinakomana ndi mmodzi wa iwo. Tsopano, Ambuye anandipatsa ine njira yodziwira zinthu. Ine ndinagwedeza dzanja lake. Ine ndinati, “Muli bwanji inu?”

Iye anati, “Iwe uli bwanji? Dzina lako ndi ndani?”

Ndipo ine ndinati, “Branham.”

“O,” iye anati, “iwe ndi mnyamata wamng’ono yemwe analalikira mmawawu.”

Ine ndinati, “Inde, wawa.”

332 Pamene ine ndinali ndikuyankhula naye, ine ndinaugwira mzimu wake. Ndipo iye anali Mkhristu weniweni, Mkhristu wangwiro basi, m'bale. Ine ndikutanthauza, iye anali wokhulupirira. Ine ndinaganiza, "O, kodi izi sizodabwitsa!"

333 Ndipo pafupi ora kuchokera pamenepo, kunja uko pafupi ndi galimoto, yomwe inkayang'anizana ndi galimoto yaikulu kwambiri, inali ndi "Yesu Yekha" zitalemba kumbuyo kwa iyo, ndipo ataima panja apo anali bambo winayo. Ndipo ine ndinatuluka ndipo ine ndinati, "Inu muli bwanji, wawa?"

334 Iye anati, "Iwe uli bwanji?" Anati, "Iwe ndi M'bale Branham, yemwe unayankhula mmawawu."

335 Ine ndinati, "Inde, wawa. Ndi ineyo." Ine ndinati, "Ndikuti, ine ndinakomedwa nazo mphatso zazikulu za Mulungu zija zomwe zimagwira ntchito mwa inu abale awiri."

336 Iye anati, "Zikomo iwe, Bambo Branham." Ndipo ine ndinayamba kuwumverera mzimu wake. Masomphenya anabwera. Ndipo ngati ine ndinayamba ndayankhulapo kwa wachinyengo, apo panali mmodzi wa iwo. Mkazi wake anali mkazi wa mutu-wakuda. Iye anali akukhala ndi mkazi wa mutu-wa bulondi, anali naye ana awiri. Iye sanali mochuluka Mkhristu moposa chinthu china mu dziko.

337 Ndiye ine ndinati, "Kodi ine ndalowa mu chiani? Ine ndimaganiza kuti ine ndinali mwa Angelo, ndipo tsopano ine ndiyenera kuti ndiri mwa ziwanda. Chinachake chachitika. Apa panali mmodzi, Mkhristu weniweni; ndipo Mzimu womwewo umagwera pa munthu *uyo*, umagwera pa munthu *uyu*." Ine ndinati, "Tsopano ine ndasokonezeka yense." Ine sindimadziwa choti nkuchita. Ine ndinalira ndi kupempha, kwa Ambuye. Ine sindimadziwa choti ndichilandire.

338 Iwo anali pafupi kuti anditengere ine ku... Anandifunsa ine ngati ine ndinali "nditalandira Mzimu Woyera?" bambo uyu anatero. Ine ndinati, "Ayi, wawa, osati momwe inu munaulandirira iwo."

Anati, "Iwe unayamba wayankhulapo mmalirime?"

Ine ndinati, "Ayi, wawa."

Anati, "Ndiye iwe ulibe Iwo."

339 Chotero ine ndinati, "Inu mwinamwake mukulondola, m'bale wanga. Mwinamwake ine ndiribe, chifukwa ine ndiribe chomwe inu muli nacho." Ndipo patapita kanthawi, ine ndinasangalala kuti ine ndinalibe.

340 Kotero ndiye ine ndinaziyang'ana izo, ndipo ine ndinawona momwe izo zinali kuyendera.

341 Chotero, tsiku lina, ine ndinali kwina kuno ndikupemphera, kale lapitalo. Ine ndikuuzani inu chifukwa chake, yemwe ine ndinali kumupempherera, anali Roy Davis. Ndipo ine ndinali

kunja uko ndikupemphera, chifukwa iye anali atanditcha ine “chidole,” ndipo ine ndinali kupemphera kuti Mulungu amukhululukire iye pa izo. Ndipo iye anali ndi malo osindikizira kuseri uko, ankalemba nyuzi. Ndipo malo osindikizira awo anagwira moto ndipo anapsya nagwa, mausiku angapo zitachitika izo, pamene iwo anali kugwiritsa ntchito icho.

³⁴² Ndipo chotero ine ndinali nditaima kumbuyo uko mu mphanga yakale kuseri kwa Chigayo cha a Green. Ine ndinayenda nkupita kumeneko. Ndipo ine ndinali kupemphera, ndinali ndiri kuseri uko, masiku awiri. Ine ndinaika Baibulo langa pansi pa chipika chakale, pamene, ine ndinamusonyeza M’bale Wood, osati kale litali, ndinaika Baibulo langa pansi. Ine ndikhala nyeng’a pa chipikacho. Ndipo mphepo inawomba. Ine ndinaganiza, “Ndakhala motalika kwambiri, umo mu mphanga imeneyo, ine ndingowerenga pang’ono.” Chotero ine ndinalitenga Baibulo ndipo ndinayamba kuwerenga, ndipo uwu unali mutu womwe ilo linali liripo. Chabwino, ine ndinayamba kuwerenga, ndipo ine ndinayamba kudabwa ndiye. Mukuona?

Pakuti ndi kosatheka kwa iwo omwe anayamba awunikiridwapo, . . . atapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera,

. . . atalawa mawu abwino a Mulungu, ndi . . . dziko likudzalo,

Ngati iwo angati agwe, kuti adzikonzenso iwoeni . . . ku kulapa; powona kuti iwo adzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu katsopano, ndi kumuika iye ku manyazi apoyera.

³⁴³ Ine ndinaganiza, “Ndi limenelo Lemba lija.” Koma chinachake chinakhalapobe ndi ine. Ndiye ine ndinayamba kuganiza, “Apa ndi pamene iye anayankhula mmbuyo umo, pachiyambi. ‘Osati kuika maziko okufa a kulapa, pa chiyambi. Osati kuika maziko a kulapa,’ ndipo apa iye akuti, ‘Katsopano, kudzikonzanso iwoeni mobwerera ku kulapa. Koma tiyeni tipitirire mpaka ku ungwiro, kuzisiya zinthu izi mmbuyo.’” Ndiye ine ndinayamba kuwerenga. Ndiye ine ndinawerenga ndime yotsatirayo.

Pakuti dziko lomwe limamwa mu mvula yomwe imadza mowirikiza pa ilo, ndi kubala zomera zoyenera iwo omwe alisamalira, limalandira madalitso ochokera kwa Mulungu:

Koma izo zomwe zimabala minga ndi zisonga ndi zokanidwa, ndipo zayandikira ku kutembereredwa; zomwe mapeto ake ndi woti zikawotchedwa.

³⁴⁴ Ndipo pamene ine ndinawerenga izo, Chinachake chinangondigwedezwa ine. Ndipo ine ndinaganiza, “Ambuye, izo si za kwa Roy Davis. Inu mungachite izo chifukwa chiyani?”

345 Ine ndinayamba, kutembenuza tsamba lina. Ine ndinachita kubwereranso kwa Ilo, kachiwiri, “Ndi zosatheka kwa iwo omwe nthawiina anawunikiridwapo,” ndinadutsa mu Izo kachiwiri.

346 Ndiye ine ndinaganiza, “Ambuye, ichi ndi chiani? Kodi Inu mukutanthauza chiani, Ambuye?”

347 Ndipo ine ndinatembenuka ndipo ndinabwerera mu mphanga yanga, kuti ndikapemphere pa Iwo. Ndipo pamene ine ndinatero, ine ndinawona dziko likuzungulira. Ndipo ilo linali lonse litalimidwa, mwabwino kwenikweni, dziko lonse. Ndipo ine ndinamuwona mwamuna atavala zoyera, akupita mozungulira, iye anali ndi thumba mu dzanja lake. Iye anali akufetsa mbewu pamene iye ankapita mozungulira. Iye anapita mozungulira kophimbika kwa dziko. Ndipo mwamsanga pamene iye anali atazungulira, apa panadza mwamuna atavala zovala zakuda kwenikweni, mwamuna wowoneka mwa ushasha, akuzembera motsatira monga *chonchi*, akuyang’ana. Ndipo iye anali ndi mbewu. Ndipo iye anali akuponyera chinachake mmbuyo mwa zija, pamene iye anali kupita akuzungulira dziko; akumuyang’ana aliyense ndi kumaponya. Ine ndinaima ndipo ndinkawayang’ana masomphenyawo.

348 Iye atapita kaye, dziko linazungulira apo, ndipo apo panali mbewu yaikulu, yochuluka, ndipo iyo inali ya tirigu. Ndipo apo panali maudzu, chisoso ndi zinthu mu tirigumo.

349 Apo panadza ng’amba. Ndipo, o, momwe tirigu wapang’ono uyo anazyolikira mutu wake wawung’onowo apo, ndipo anali ndi ludzu la madzi. Chisoso chaching’ono chinali ndi mutu wake wawung’ono utazyolitsidwa, ndipo icho chinali ndi ludzu lofuna madzi. Aliyense anali akupemphera kufuna mvula. Ndipo patapita kanthawi, motsatira kunadza mtambo waukulu ndipo unangotsirira dziko lonselo. Ndipo chisoso chaching’ono chinalumphira mmwamba, nkuyamba kufuula, “Ulemerero kwa Mulungu! Aleluya! Mulungu alemekezeke!”

350 Ndipo tirigu wapang’onoyo, iye analumphira mmwamba, nayamba kufuula, “Ulemerero kwa Mulungu! Ambuye alemekezeke!”

351 Ndiyeno Lemba linadza kwa ine, lomwe limapezeka mu Bukhu la Mateyu, mutu wa 5 ndi ndime ya 45. Ndipo mvetserani kwa zomwe Yesu ananena, mu Mateyu 5:45. Ndipo mvetserani mwatcheru tsopano pamene ife tikuwerenga. Mateyu, mutu wa 5 ndi ndime ya 45, 46; ya 44, kuti tiyambirepo.

Koma ine ndikuti ndi inu, Kondani adani anu, adalitseni iwo omwe akutukwanani inu, ndipo chitani zabwino kwa iwo omwe akudani inu, ndipo ziwapemphererani iwo omwe akugwiritsani ntchito inu monyozetsa, ndi kukuzunzani inu;

Kuti inu mukhoze kukhala...kutchedwa...inu mukhoze kukhala ana a Atate anu omwe ali kumwamba:

*pakuti iye amapangitsa dzuwa lake kuwalira pa...
oyipa ndi pa...abwino, ndipo amatumiza mvula pa
olungama ndi...osalungama.*

³⁵² Chotero, inu mukuona, mvula yomweyo imene imapangitsa tirigu kumera, imapangitsa chisoso kumera. Ndipo, chotero, ine ndinachigwira chithunzicho. Ndi uyo wovomereza wanu mwachithupithupi, umo ndi mu mpingo momwe. Koma zipatso zake...Iye akhoza kufuula, kulumpha, kuvina, kuyankhula ndi malirime; koma zipatso zake: iye ndi chisoso. Ndipo ndi uyo winayo, yemwe ali ndi Mzimu womwewo. Mzimu Woyera ukhoza kugwera mu gulu la anthu momwe, ndipo wachinyengo akhoza kufuula, mwa Mzimu Woyera, mofanana basi monga chisoso chingakhalire moyo ndi mvula yomwe itumizidwa. Ndi zomwe Paulo akuziyankhula apa. Koma ndi kosatheka kuti chisoso chikhale tirigu, kapena tirigu kukhala chisoso. Inu mukuzimvetsa izi? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

*Pakuti ndi kosatheka kwa iwo omwe anayamba
awunikiridwapo, ndipo a...anagawana nawo za
mphatso ya Mzimu Woyera,*

*Ndipo...analawa mawu abwino a Mulungu, ndi
mphamvu ya dziko liri nkudza,*

*...kuti agwere kumbali, kuti adzikonzenso iwookha
kachiwiri...*

Mvetserani zomwe iye ananena.

*...pakuti mvula...imadza mowirikiza pa dziko
lapansi, kuti itsirire ndi kulisamalira ilo kuno, ndi
kulikonzeketsera ilo;*

*Koma...zomwe ziri minga ndi nthula ziri pafupi kuti
zikanidwe;...*

*Tsopano, chotero posiyana nazo zoyambirira ndi
ziphunzitso za Khristu, tiyeni ife tipite...ku ungwiro;
osati kuyika kachiwiri maziko a kulapa ndi ntchito
zakufa...kwa Mulungu, ndi chikhulupiriro, ndi zina
zotero,*

*...ndi ziphunzitso za maubatizo,...kuika kwa
manja, ndi zinthu,...*

³⁵³ Mukumuona, wokhulupirira wachithupithupi, mmbuyo mu masiku amenewo, monga momwe iye aliri lero, anakonda kunena kuti, "Chabwino, ndine wa mu mpingo. Ine ndalapa. I—ine ndinabwera kuno, ine ndinapanga kuvomereza. Ine ndinabatizidwa." Mukuona, iwo amatsamira pa kukonzanso kwachithupithupi uko. Ndipo kodi izo zimachita chiani? Izo zimabala zisoso.

³⁵⁴ Kodi ungwiro umachita chiani? Ndiye tiriguyo. Tirigu ndi Mawu a Mulungu. Iye amamugwiritsa ntchito iye monga Mawu Ake. Iwo ndi Mbewu. Iwo amabala apo.

³⁵⁵ Izo zimatengera mbewu yomwe inafesedwa mu mtima mwanu. Ngati inu mumabwera ku mpingo basi chifukwa kuti inu mukuwopa gehena, ngati inu mukujoyina mpingo chifukwa kuti inu simu—simukufuna kuti mudzapite ku gehena, inu mukadali chisoso. Ngati i—ngati inu mujowina mpingo pongofuna kuti mutchuke, inu mukadali chisoso. Ngati inu munachita zinthu zonse zamawonekedwe izi zomwe ziri zoti zizichitidwa, ndipo izo ndi zonse zomwe inu muli nazo, inu mukadali chisoso.

³⁵⁶ Koma Mkhristu weniweni, woona amalimbikira kumka ku ungwiro mpaka dziko litafa ndipo inu mwakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu. Ndiye, ndi kosatheka kuti munthu ameneyo adzagwe konse. Nzomwe Baibulo linanena! Mukuona momwe izo zikufananirana ndi Lemba lonselo? Mukuona momwe Ilo likuikira izo pa malo ake?

³⁵⁷ Kodi Izo zinganene motani apa, “Munthu yemwe anayamba wapulumutsidwapo sangakhoze konse kutaika” ndipo nkubwera apa ndi kuti, “Koma, ngati iwe wataika, kapena wachitiramwano, ndi zosatheka”? Zedi, ngati iwe uli wochitiramwano, sindiwe Mkhristu ayi.

³⁵⁸ “Palibe munthu, woyankhula mwa Mzimu wa Mulungu, angamutche Yesu kuti ndi wotembereredwa.” Yohane Woyera 4. . . kapena Yohane Woyamba 4. Palibe munthu woyankhula mwa Mzimu wa Khristu, angamutche Yesu “wotembereredwa.” Mzimu uliwonse, wa Mulungu, umene uli mu Mpingo wa Chikhristu, umagwirizana ndi chirichonse chomwe Mulungu ananena.

³⁵⁹ Iye timawerenga apa, ndi kuti, “Iye anavulazidwa chifukwa cha mphulupulu zathu. Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.”

³⁶⁰ Malingaliro okalamba achithupithupi amati, “Masiku a zozizwitsa anapita. Ine ndine *Dr. Jones*.” Mukuona? “Palibe chinthu chotero ngati machiritso Auzimu. Palibe chinthu chotero monga chipembedzo chokukhudza mu mtima. Ndinu basi gulu la odzipangitsa. Ndinu otengeka. Mukuona, ndizo zonse zomwe ziri kwa izo. Palibepo kanthu kwa izo. Ndife Achipresbateria. Ndife Achilutera,” kapena chirichonse chomwe icho chiri. “Ife tikudziwa pamene ife tiri kuima.”

³⁶¹ Koma kodi Mzimu wa Mulungu umati chiani? Yesu Khristu, yemweyo pano! “Ameni,” umatero Mzimu wa Mulungu. Iwo umagwirizana mofulumira ndi Mawu. Inde, bwana. Iwo uli apo pomwe. Mukuona zomwe ine ndikutanthauza tsopano?

³⁶² “Kukonzanso kwa chithupithupi uku kumapanga imfa,” anatero Paulo.

³⁶³ Koma komwe Moyo wabwera, ungwiro uwu, “Iye amene amva Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzabwera konse ku

kuweruzidwa, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Ine ndidzamupatsa iye Moyo wosatha, kumuukitsa iye mu masiku otsiriza. Onse omwe Atate anandipatsa Ine adzaza kwa Ine, ndipo palibe mmodzi wa iwo wotaika.” Sangati akhale.

³⁶⁴ Chotero, apa pali zomwe izo zimachita—chomwe izo zimachita. Anthu amaganiza kuti izo zimawapangitsa anthu kutairira. M’bale, inu simumamutumikira Mulungu pansi pa kuwopsyeza kwa serpenti. Mulungu si mmodzi wa amuna awa okhala ndi chikwapu cha njoka yakuda, kumakuongolerani inu kulikonse. Iye ndi Atate. Iye ndi Chikondi. Mulungu ndi Chikondi. Ndipo Baibulo linatero, mu Yohane Woyera, “Iye amene amakonda ndi wa Mulungu.”

³⁶⁵ Inu mumamukonda Mulungu. Ine sindikanati ndikhale, ngati ine ndikanapita kunja n—ndi kukaledzera usikuuno. Ine sindinayambe ndamwapo, mu moyo wanga. Koma ngati ine ndikanapita ndi kukaledzera, ine sindikanati ndichite mantha ndi kukwapulidwa. Icho si chifukwa chomwe ine sindimapita—kupita, sindimapitira kukachita izo. Chifukwa chomwe ine sindimapita kukachita izo, ndi chifukwa ine ndimamukonda Iye. Iye amandikonda ine. Izo si ntchito za lamulo. Izo si chinachake chomwe ine ndikuyenera kuti ndizichita. Ndi chifukwa Iye anandichitira kale ine chinachake, ndipo ine ndimamukonda iye chifukwa cha izo. Ndi zimenezotu.

³⁶⁶ Chotero, ndi Mzimu umenewo mmenemo, umene unalonjezedwa, “Ine ndimapereka kwa iye Moyo wosatha, ndipo iwo sadzawonongeka konse.” Kodi Iye ananama kapena Iye anatiuza Choonadi? Iye anatiuza Choonadi. Chotero, inu mukuona momwe Izi zikutanthauzikira? Chosatheka ndi kuti munthu agwe iye atakhala kale mu chisomo. Iye sangakhoze. Iye akhoza kugwa, zedi, koma osati koti alape, kubwerera ku malo ndi kumakachita ntchito zakale mobwereza kachiwiri.

³⁶⁷ Chotero, inu nonse mukungonyang’ama kuchokera ku chitsitsimutso kupita ku chitsitsimutso, malo amodzi ndi kenako ena, kodi inu simukuwona kuti inu si odekha? Inu si okhazikika. Tsopano, ndithudi. . . Inu mukuti, “M’bale Branham, ine sindikudziwa ngati. . .” Ndithudi Mulungu sangandipatse ine utumiki umene Iye ali nawo, ndi kundisiya ine kuti ndikhale mu kulakwitsa. Ndipo izo zikanati zisamatsimikiziridwe ndi Lemba, ndiye izo zikanakhala zolakwitsa, koma apa pali Lemba loikira izo kumbuyo.

³⁶⁸ Mipingo sinaphonye konse malo. . . Anthu amapita, kukajowina mpingo, kukangana, kumenyana, kulundirana, n—ndi chirichonse, ndi kumangokhala mtundu uliwonse wa moyo wachithupithupi, “O, inde, ndine Mkhristu.”

³⁶⁹ Ine ndinamva chivomerezo lero cha dona wamng’ono yemwe amandiuza ine kuti mwamuna wake amathamanga ndi

mwamuna. Iye wawagwira iwo, malo ndi malo. Ndipo mkaziyo akuti, “Ine ndikuti ndikudziwitseni inu kuti, ‘Ndine Mkhristu.’”

³⁷⁰ Tayang’anani cha kuno Jimmy Osborne, kunja kuno akulalikira Lamlungu mmawa; ndi kwasa-kwasa, gwedemula ndi chirichonse, podutsa mu sabata.

³⁷¹ Tayang’anani pa Elvis Presley, mchitidwe wa 1947 wa Yudasi Iskariote, analowa Assemblies of God, Wachipentekoste, woyankhula mu malirime a Mzimu Woyera, ndipo watumiza miyoyo yochuluka kokazunzidwa kuposa malo onse omwera mowa omwe akhalapo mu zaka makumi asanu zapitazi. Wapotoza malingaliro a ana a zaka za mmatini konsekonse mdziko, mpaka asungwana aang’ono akhoza kugwira zovala zawo zamkati ndi kuzichotsa kuziponyera izo pa nsanja, kuti iye asayinepo. Zauve kwambiri mwakuti iwo sangamuwonetse iye pa kanema, kuyambira mchiuno mwake kupita mmusi, liriri thupi lakelo. Mzimu Woyera, woyankhula mmalirime, ngati umboni? O, m’bale, ngati Mzimu Woyera unali mmenemo, Iwo sukanati uzichita monga choncho. Inu mukudziwa bwinoko kuposa izo. Ndithudi ayi. Mulungu amakonda ukhondo ndi ungwiro ndi chihero.

³⁷² Ine sindimadzipangitsa kukhala waukhondo ndi wangwiro ndi woyera kuti ndidzipange ndekha kukhala Mkhristu. Koma Khristu, mkati mwa ine, amakhala moyo zimenezo mkati mwa ine. Ndipo ine ndimamukonda Iye. Ndipo ngati ine ndichita chirichonse cholakwika, icho chimanditsutsa ine, apo pomwe. Ine ndimati, “Mulungu, ndikhululukireni ine.” Tsiku lililonse, ine ndimayenera kupempha chikhululukiro, tsiku lililonse. Ndipo inu mumatero, nanunso. Ndithudi, inu mumatero.

³⁷³ Koma tsopano ngati inu—ngati inu muli wachithupithupi, inu mumangodikirira mmbuyo, nkuti, “Aha, chabwino, izo ziri bwino, ndine wa mpingo.” Mukuona? Ndiyeno pamene inu muchitira mwano, ndi pamene inu mulibe Chikhulupiriro chomwe chinaperekedwa poyamba kwa oyera. Ndiye inu mumaunyogodola Iwo, ndi kuwutcha Iwo, “Mzimu woipa.” Nkuti, “Ilo ndi gulu la oyera-odzigudubuza.” Ndiye, inu mumadzilekanitsa nokha pakati pa chisomo ndi chiweruzo, ndiye inu mwathedwa kwanthawizonse.

³⁷⁴ Yesu anati, “Mawu amodzi otsutsa Iwo, izo sizidzakhululukidwa kwa inu konse mu dziko lino kapena dziko likudzalo.” Ndipo Mkhristu, wobadwa ndi Mzimu, sangakhoze kunena choipa za Iwo, chifukwa izo sizingatheke. Iwo amagwirizana ndi Uwo. Ndiko kulondola.

³⁷⁵ Ndi chifukwa anthu akuyesera kundiuza ine, Lawi la Moto ilo apo, lomwe likuwoneka pano liri ndi ife, iwo akuyesera kumanena, kuti, “Ameneyo anali Mdierekezi,” kuti, “Izo zinali zopeka basi,” zonse izi. Koma kamera inatsimikizira kuti Izo sizinali. Ndipo ntchitozo ziri bwinobwino ndendende mwa

Baibulo, Lawi la Moto lomwelo limene linakomana naye Paulo ali panjira yaku Damasko. Zinthu zonse izi zomwe Iye anazichita mmbuyomo uko, akuchita izo ndendende basi njira yomweyo, mwa Baibulo. Iye ndi Khristu, Mwana wa Mulungu.

³⁷⁶ Ndipo pamene ife tibadwa kachiwiri, ife tiri nawo Moyo wosatha, ndipo sitingakhoze kuwonongeka. Zingakhale ziri zosatheka kuti munthuyo agwe. Ndi chimene Baibulo linanena.

³⁷⁷ Tsopano, mvetserani, penyani zomwe Paulo akunena. Ine ndiwerenga zonse za izo, ndi kuwona ngati izo sizikumveka molondola, tsopano. Tiyeni tipitirire nazo, miniti yokha. Ndime ya 8.

Koma zomwe zibala minga ndi nthula zimakanidwa, ndipo zimayandikira ku kutembereredwa; zomwe mapeto ake ndi kuti ziwotchedwe. (Uyo ndi wosakhulupirira.)

³⁷⁸ Tsopano penyani Paulo. “Koma, okonedwa, . . .” Tsopano iye akukamba za iwo omwe akuyesera kuti abwerere pansu pa lamulo, inu mukudziwa, akuyesera kuti azichita ntchito zonse kudzera mu lamulo, komabe iwo ali amwambo monga iwo angakhoze kukhalira. Iwo ali nawo maubatizo ndi kuikapo kwa manja, ndi zinthu zonse izi.

Koma, okonedwa, ife tiri okakamizidwira zinthu zabwinoko za inu, . . .

Ndi inu apo. Mvetserani kwa iye tsopano.

. . . ndi zinthu zomwe ziri kutsatira chipulumutso, ng—ngakhale kupyolera mu izi ife tayankhula chotere.

Pakuti Mulungu si wosalungama kuti aiwale ntchito zanu ndi kuvutikira kwa chikondi, zomwe inu mwasonyezera kwa dzina lake, mmenemo inu mwatumikira kwa oyera, ndipo muli kutumikira.

³⁷⁹ Mukuwona zomwe Iye akuzinena? Iye Sali kuyankhula za Akhristu kugwera kwina, kusatheka kuti abwererenso. Iye akuyankhula za okhulupirira achithupithupi omwe amadutsa mu mawonekedwe a kukonzanso. “Koma,” iye anati, “kwa inu omwe munabadwa kachiwiri, inu omwe muli Mkristu, wokonedwa, ife tiri okakamizidwira zinthu zabwinoko za inu. Inu simumanena zinthu zimenezo. Inu simumakhala moyo wa mtundu umenewo. Ndinu otetezedwa ndi Khristu.”

Kodi iye ananena chiani mmbuyo umu? Tsopano tiyeni tipite ku Ahebri 10, pamene ife tinali mmawa uwu, kachiwiri. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

³⁸⁰ Tsopano tiyeni titembenuze ndiye, kachiwiri, ku Aefeso 4:30. Ndipo tiyeni tizitenge izi, miniti yokha, ndi kupenya zomwe iyo ikunena, kuti tiikire kumbuyo izi, kuti tilipange Lembha kumapita limodzi ndi Lembha. Aefeso 4, tiyeni tiwone.

Aefeso 4:30. Tiyeni tiwerenge ndi kuwona zomwe Ilo likunena. Mvetserani.

...musati muwukwiyitse Mzimu woyera wa Mulungu,...

Aha? Ife timabatizidwira chotani mu Thupilo? Mzimu Umodzi.

...musati muwukwiyitse Mzimu woyera wa Mulungu, womwe inu mumasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.

Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mumasindikizidwira mu Thupi la Khristu, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, osati kuchokera ku chitsitsimutso chimodzi kupita ku chimzake, koma mpaka Tsiku la thupi la chiwombolo. Ndicho chimene inu muli. Koteru, palibe njira yomwe inu mungati mutaikire.

³⁸¹ Inu mukuchita mantha. Ndipo ndi chifukwa mantha, mantha, kuwopa kumatsatana ndi kukaikira.

Chikondi chimatsatana ndi chikhulupiriro. Ine ndimawakonda Atate anga. Ine sindimawawopa Iwo, chifukwa ine ndimawakonda Iwo. Iwo sangandipweteke ine. Iwo angandichitire ine zabwino. Ngati ine ndikanakhala wowawopa Iwo, ndi, “O, ine sindikudziwa ngati Iwo ati azichite izo, kapena ayi.” Mukuona?

³⁸² Koma ngati ine ndimawakonda Iwo, “Inde, Atate, i—ine ndimakukondani Inu. Ndipo ine ndikudziwa Ndinu—Ndinu Atate anga, ndipo Inu mumandikonda ine, ndipo ine sindiri kuchita mantha koma kuti Inu muzisunga Mawu Anu. Ndi lonjezo Lanu kwa ine.” Umo ndi momwe Mzimu wa Mulungu umachitira.

³⁸³ “Koma, o, ngati ine ndikanachita *izi*, ngati ine ndikanachita *izo*.” Mukuona, apo inu mwabwera ku mbali yalamulo, kachiwiri. Musamapite konse ku mbali yalamulo. Ndi yolepheretsa.

³⁸⁴ Mbali yokhoza ndi yomwe inu mukuifuna. Iyo ndi ntchito yotsirizidwa kale. Khristu anafa, ndipo tchimo linaphedwa pamene Iye anafa. Ndipo ngati Mulungu anakudzozeranitu inu ku Moyo Wamuyaya, “Onse omwe Atate anandipatsa Ine, adzadza kwa Ine.” Ndi inu apo, sangakhoze kutaika. Ndinu otetezeka kwanthawizonse. “Pakuti ndi Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndipo mwa nsembe imodzi Iye anatipanga ife kukhala angwiwo kwanthawizonse.” Ndi inu apo. Palibe njira yomwe ife tingaluzire. Kulondola. Tsopano, kodi izo sizikukupangani inu kumverera bwino? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

³⁸⁵ Tsopano, inu mungadziwe bwanji kuti ndinu Mkhristu? Pamene mzimu wanu uchitirana umboni ndi Mzimu Wake,

pamene chikondi cha Mulungu chiri mu mtima mwanu, pamene inu muli ndi chikondi, chisangalalo, mtendere, kuvutika motalika, unjonda, chipiriro, ubwino, kufatsa. Ndi pamene inu. . . Zipatso za Mzimu zikuwutsatira moyo wanu.

³⁸⁶ Osati chifukwa choti inu mukhoza kuvina mu Mzimu, o, kwa mayimbidwe amakono awa, kuithabwanya iyo pa limba, kwa ochuluka a awa pano ovina mu Mzimu. Zinthu zimenezo ndi zabwino bwino. Koma iwo anatengera chinthu chonsecho ku mbali yalamulo iyo, mukuona, ndipo chotero, iwo anawusiya Mzimu wa Mulungu mmbuyo.

³⁸⁷ Ndicho chifukwa, pamene Mulungu anayamba kudziwonetsera Iyemwini, iwo anati, “Zachabechabe. Ife sitikufuna kalikonse kochita ndi Zimenezo.” Iwo samamudziwa Mulungu. Iwo sanayambe aziwonapo Izo. Iwo sangathe kuzimvetse Izo, chifukwa muli moyo wosiyana mmenemo. Iye sakudziwa. . . Chisoso sichimadziwa chomwe tirigu akuchita. Iye ali moyo wosiyana.

³⁸⁸ Umo ndi momwe ziriri ndi Mkhristu, kwa wokhulupirira wa chithupithupi, wodzinenera, yemwe amapita ndi kumakanena, “O, inde, ndine Mkhristu.” Chindudu chachikulu mkamwa mwake, monga ng’ombe yopanda nyanga yaku Texas.

³⁸⁹ Mkazi atavala kabudula wake, nkumati, “O, inde, ndine membala wa mpingo. Zedi, ine ndiri.” Zipatso zako zikutsimikizira kuti sindiwe kanthu koma wachithupithupi. Ndiko kulondola. Ndithudi, izo ziri. Pali chinthu chimodzi chokha choti chivomereze zimenezo: ndizo mwina kuperewera kwa ubongo kapena mzimu wa kusilira uli pa iwe. Ndiko kulondola.

³⁹⁰ Ngati inu mukufuna kuti muzichita monga dziko, Baibulo linati, “Ngati inu mukonda dziko kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.” Kotero ndi inu apo.

³⁹¹ Tsopano, inu mukuti, “O, Baibulo linatero, ndiye ine ndiyenera kuti ndizichita izo.” Ayi, sindizo. Zikhalani apa mpaka Khristu atakuchitirani inu chinachake, chimene chingazichotse izo mwa inu. Ndiye ndinu obadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Osati zomwe inu muchita, ndi zomwe Iye anakuchitirani inu. Mpaka inu mutapeza chikondi choti inu mwadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Ndiyeno muwuyang’ane moyo wanu, ngati i—ngati iwo ukugwirizana nazo. Osati chifukwa inu mukuyesera kuupanga moyo wanu, koma chifukwa Mulungu akukufikitsani inu mu kumvera kwa Mzimu Wake. Si inuyo kudzitsogolera nokha mu njira ya Mulungu. Ndi Mulungu kumakutsogolerani inu munjira Yake Yomwe. Osati inuyo kumachita kutsogolerako, koma Mulungu kumachita kutsogolerako.

392 Tsopano penyani izi, tsopano, basi pamene ife tikufika cha ku mapeto. Ndime ya 11.

Ndipo ife tikukhumba kuti aliyense wa inu aziwonetsera changu chomwechi mpaka ku chitsimikiziro chathunthu cha chiyembekezo kufikira chitsiriziro:

Kuti inu musakhale aulesi, koma otsatira iwo amene kupyolera mu chikhulupiriro ndi chipiriro akulandira lonjezo.

393 Tsopano, ndemanga imodzi ina yokha apa.

Pakuti pamene Mulungu anapanga lonjezo kwa Abrahamu, chifukwa iye sakanakhoza kulumbira pa wamkulu wina aliyense, iye analumbira pa iyeyekha,

Nati, Ndithudi kudalitsa ndidzakudalitsa iwe, ndipo kuchulukitsa, ine ndidzakuchulukitsa iwe.

394 Pamene Mulungu anakomana naye Abrahamu! Tsopano, Abrahamu analandira pangano, popanda kuyenera kulikonse nkomwe. Pangano linapangidwa limodzi ndi Abrahamu. Zinali mwamtheradi chisomo, mwapalimodzi. Abrahamu sanali munthu wabwinoko. Iye sanali munthu wachiyero. Iye anangokhala munthu wamba. Ndipo Mulungu, mwa kusankha, anamusankha Abrahamu chifukwa Mulungu anamusankha iye; osati chifukwa Abrahamu ankazifuna izo, chifukwa Abrahamu anachita *ichi*, chifukwa iye anali munthu wabwino, chifukwa iye anali ndi kuyenera kulikonse nkomwe. Koma uko kunali kusankha kwa Mulungu. Mulungu anamutenga Abrahamu.

395 Lero, monga ine ndinanena, ine ndikukhulupirira, “Ife timasankha azilaliki athu.” Ife timayenda yenda, nkuti, “Chabwino, mmodzi wa madikoni wasiya. Tiyeni tipeze munthu wabwino kwambiri mu chipinda chino kuti atenge malo ake. Chabwino, abusa asiya; tiyeni tifufuze, ife tipeze wabwino kwambiri.” Nthawizina izo si zokhoza.

396 Pamene iwo anamusankha munthu woti atenge malo a Yudasi, iwo anatenga munthu wolakwika. Iwo anatenga njonda, Matiya, mlembi wamkulu, sikolala, nthumwi. Iwo anati, “Iye angotenga malo enieniwo. Mnyamata, iye akuwoneka ngati mwamuna weniweni.” Koma uko sikunali kusankha kwa Mulungu. Ndipo iye anamutenga munthu uyu, ndipo iye sanachite kanthu kalikonse kwa Mulungu.

397 Koma Mulungu anatenga kusankha kwa ka, Myuda kachikulire kakupsya-mtima, ka mphuno yangowe komwe kanachokera uko. Nkhope yake, yonse, “Ine ndipita uko. Ine ndikawamanga iwo.”

398 Mulungu anati, “Ine ndikuwona chinachake mwa iye. Ine ndimugwiritsa ntchito iyeyu.”

399 Ndipo Mulungu anawonekera pamaso pa iye, Kuwala kwakukulu kuja uko. Ndipo iye anati, “Ndinu yani, Ambuye?”

400 Anati, “Ndine Yesu. Bwanji, ndi kovuta kuti iwe uzimenyana ndi zisonga. Chifukwa chiani iwe ukundizunza Ine?” Monga chomwecho, ndipo Mulungu anamutenga munthu *ameneyo* ndipo anamupanga iye mmodzi wa amuna aakulu kwambiri omwe anayamba agunda pa nkhope ya dziko lapansi chichokereni Yesu Khristu. Uko kunali kusankha kwa Mulungu.

401 Lero, ife tikuyesa kupanga kusankha. Inu mipingo, inu mumamutumiza munthu *uyu* kuno, ndi munthu *uyo* kuno. Izo sizimayenera kuti zizichitidwa mwanjira imeneyo. Mulungu amachita kutsogolerako. Ndi Mulungu mwa onse, kupyolera mwa onse, pamwamba pa onse; osati zomwe zipepala zina za mpingo wina. Ndi zomwe Mulungu ananena pa izo, zomwe zimapangitsa kusiyana.

402 Zindikirani. Mulungu anapanga lonjezo kwa Abrahamu, lopanda mangawa. Ndipo tsopano, dikirani, Abrahamu sanasowe kuti achite chinthu chimodzi. Mulungu anati, “Ine ndazichita kale izo.”

403 Mulungu anapanga lonjezo kwa Adamu, anati, “Adamu, ngati iwe sudzakhudza *ichi*, iwe udzakhala moyo kwa nthawizonse. Koma tsiku lomwe iwe udzadye za mmenemo, tsiku limenelo iwe udzafa.”

404 Adamu anati, “Ine ndikungodabwa kuti zonsezi ndi chiani, mulimonsebe?” Iye akupita ndi kukadya icho, kupulupuza.

405 Nthawi iliyonse yomwe Mulungu apanga...munthu amapanga pangano lake ndi Mulungu, kapena Mulungu ndi munthu, munthu amaswa gawo lake. Chotero Mulungu anayenera kuchita chinachake, chifukwa Iye anawona chimene munthu anali. Ndipo iwo anadzozedweratu, iwo anasankhidwa, ndipo Mulungu anayenera kuchita chinachake. Chotero Mulungu anabwera pansu ndipo anapanga pangano Lake ndi Abrahamu, mopanda mangawa. Ngati ilo likanati lisakhale lopanda mangawa, Abrahamu mwenzi atataika, nthawi yapakale.

406 Tayang’anani pa iye atakhala pansu kuja ku Gerara, wobwerera mmbuyo, akunena bodza. Ndipo anampereka mkazi wake kwa mwamuna wina, kuti apulumutse khungu lake lomwe. Mwamuna wotani! Atakhala panja paja, ndipo ali wobwerera mmbuyo. Mulungu anamuza iye, anati, “Usati uchokeko kuno, zikhala komwe kuno.” Njala inamuthamangitsira iye kwina. Iye anayendayenda mpaka komwe kunali kophwekera kupitako. Inu mukudziwa zomwe zimachitika kwa munthu pamene iye atenga njira yophwekerapo.

407 Iye anakayendayenda kwina, kumusi uko kumene msipu unali wobiriwirapo. Ndipo pamene iye anakafika kumusi uko, iye anamuza mfumu uja kuti mkazi wake anali “mlongo”

wake, kuti apulumutse khungu lake lomwe. Tsopano, limenelo linali bodza. Ndipo, mwamuna aliyense, angatenge mkazi wake ndi kumupereka iye kwa mwamuna wina, kuti apulumutse khungu lake! Apo iye anali, atakhala panja apo mu hema wamng'ono, wobwerera mmbuyo, akunena bodza, ndipo atachoka kwathunthu ku zake, atadzidula palimodzi nazo nachoka ku lonjezo ndi chirichonse, koma iye anali akadali mneneri wa Mulungu.

⁴⁰⁸ Ndipo apo panali Abimeleki, iye anali munthu wabwino, wachiyero. Zedi, ankanena mapemphero ake usiku uliwonse. Anamupeza gogo wamkazi uyu, wa usinkhu wa zaka zana, akubwera kumusi uko, wokongola ndipo ali wamng'ono kachiwiri. Iye anati, “Uyo ndi msungwana yemwe ine ndakhala ndikumuyembekezera, chotero ine ndingopita kukamukwatira iye.”

⁴⁰⁹ Abrahamu anati, “Iwe ukhoza kumutenga iye. Iyeyu ndi mlongo wanga.”

Iye, “Uyo ndi mchimwene wanga.”

⁴¹⁰ Chotero iye akumutengera iye uko ndipo ali ndi akazi oti akamusambitse iye yense n—ndi kumuveka zovala zabwino, ndi kumukonza iye m—monga mfumukazi. Ndipo iye ananena mapemphero ake, anadzilambatitsa pa kama, ndi kutembuzira miyendo yake mmwamba, ndipo anati, “Mawa, ine ndimukwatira msungwana wa Chihebri wokongola uyo, mlongo w—wake wa mnyamata uyo ali ukoyo. O, izo zikhala ziri zodabwitsa. O Ambuye, Inu mukudziwa momwe ine ndimakukonderani Inu! Inde, bwana. Zodabwitsa!”

⁴¹¹ Ndipo Mulungu anati, “Iwe uli basi ngati munthu wakufa.” U-nhu!

[“M'bale Branham akutsokomola—Mkonzi.”] Ndikhululukireni ine. Abra- . . .

⁴¹² Pakuti, Abrahamu anali atakhala cha kumeneko, bodza, ndi wobwerera mmbuyo. Ndipo apa panali munthu uyu, woonamtima ndi wolungama ndi mwamuna woongoka. “Pakuti,” iye anati, “Ambuye, Inu mukudziwa luntha la mtima wanga. Kodi iye sanandiuze ine, kuti uyo anali ‘mlongo’ wake?”

⁴¹³ Anati, “Ine ndikudziwa luntha la mtima wako. Ndi chifukwa chake Ine ndikukuteteza iwe kuti usandichimwire Ine. Ndiko kulondola. Ine ndikudziwa luntha la mtima wako. Koma mwamuna wake ndi mneneri Wanga.” Aleluya! O, ngati icho si chisomo, ndi chianino? “Atabwerera mmbuyo, akunena bodza, ndipo atakhala kwina uko, koma uyo apobe ndi mneneri Wanga. Iwe utenge chopereka, ndipo upite kwa iye, ndipo iwe ukamubwezere mkazi wakeyo, kapena ndiwe munthu wakufa. Ine sindimvanso mapemphero ako kenanso. Ukamulole iye akakupempherere iweyo.” Ameni. Ndi inu apo. “Ameneyo ndi mneneri wanga.”

Tsopano, inu mukuti, “O, ine ndikukhumba ine ndikanakhala Abrahamu.”

⁴¹⁴ “Ngati ife tiri akufa mwa Khristu, ife ndife Mbewu ya Abrahamu, ndipo ndife olandira nawo molingana ndi lonjezo.” Kulondola. Ndi chimene Baibulo linanena. Kodi inu mukanafuna kuti muziwerenge Izo? Pakuti, Baibulo linanena izo, kuti lonjezo limenelo silinali kwa Abrahamu yekha ndi mbewu zake. Monga inu, Abrahamu anali nazo mbewu zambiri, zedi, ana ambiri. Ishmaele anali mwana wake. Iye anali nawo ana asanu ndi awiri kapena asanu ndi atatu Sara atamwalira, ndi winawake, Keturah. Koma, penyani, mbewu inali yolonjezedwa iyo, yomwe inali Isaki, ndipo kudzera mwa Isaki kunadza Khristu, kudzera mwa Khristu tinadza ife. Lonjezolo ndi la mopanda mangawa.

⁴¹⁵ Tsopano, nanga bwanji Abrahamu? Pakuti, iye akanakhala atathedwa, sikukanakhala kuli kotheka kuti iye akhoze kubwerera kachiwiri konse. Zedi. Sikukanakhala kuli kotheka kuti Sauli abwerere konse kachiwiri, ngati izo, inu mukanati muziwerenga Lemba mwanjira imeneyo. Mukuona? Koma izo sizinali. Lonjezo la Mulungu limapitirirabe kwanthawizonse.

⁴¹⁶ Tiyeni tiwerenge apa miniti yokha. Ine ndikufuna kuti inu muwerenge Izo. Ine ndikufuna kuti inu mutenge Agalatia 3:16, ndi kuwerenga izi, ndipo muwone tsopano chomwe lonjezolo liri, ndi kuwona chomwe n—ngati ife tiri lonjezo Lake kapena ayi, 3:16. Mvetserani apa. Chabwino. Ine ndikuti ndiwerenge ndime ya 15, nayonso.

Abwenzi, ine ndikunena monga kachitidwe ka munthu; Ngakhale pangano liri koma la munthu, komabe ngakhale ilo litatsimikiziridwa, palibe munthu aliyesa lachabe kapena kuonjezera pamenepo.

Tsopano kwa Abrahamu ndi mbewu yake, mbewu (m, b,e,w,u.), kwa mbewu yake lonjezo linapangidwa.

“Kwa Abrahamu ndi mbewu yake.” Tsopano penyani.

Iye sakunena kuti, Ndi kwa mbewu zako (zambiri), ngati zambiri; koma monga . . . imodzi, Ndi kwa mbewu yako, yomwe ili Khristu.

⁴¹⁷ Ndiye, Khristu anali Mbewu ya Abrahamu. “Ndipo ife pokhala akufa mwa Khristu, ndipo titabatizidwa kulowa mu Thupi Lake, ife tiri Mbewu ya Abrahamu, ndipo ndife olandira nawo lonjezolo.” Ndiye ziri motani, inu mudzagwera kwina konse chotani, ngati Mulungu anapanga lonjezo kwa inu? Inu mudzabwerera mmbuyo konse chotani, ndi kuchokapo ndi kuchita kupita ku gehena chifukwa cha izo?

⁴¹⁸ Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, kodi ife sitingabwerere mmbuyo?” Mwamtheradi. Ndipo pamene inu mubwerera mmbuyo, inu muzilandira izo, inu musati mudandaule.

Abrahamu analandira izo, ndipo ena onse a iwo analandira izo, ndipo inu mulandira izo. Inu musati muganize kuti izo zikukupatsani inu ufulu woti muzichimwa. Izo siziri. Inu mudzalipira pa chirichonse chomwe inu muchita. Inu mudzakolola chomwe inu mubzala. Inu mukachita katchimo kamodzi kakang'ono ndipo inu mudzakolola zodzadza msambidwe yonse. Ndiko kulondola. Koma, m'bale, izo sizikutanthauza kunena kuti iwe wataika. Ndiko kulondola ndendende. Abrahamu anakolola ndendende zomwe iye anafesa. Ndiko kulondola. Koma iye anali apobe wopulumutsidwa.

⁴¹⁹ Pangano lomwe Mulungu anapanga ndi Israeli: iwo anataya cholowa chawo, iwo anataya dziko lolonjezedwa ndipo anapita uko ku Igupto, koma iwo anali asanataye pangano lawo. Mulungu anati, “Ine ndakumbukira lonjezo Langa kwa Abrahamu. Ine ndakumbukira, ndipo Ine ndabwera pansu kuti ndidzawawombole anthu Anga. Pita komweko, Mose, ndi kukamuza Farao, Ine ndati, ‘Asiye anthu Anga apite.’ Ine ndakumbukira kuti Ine ndinapanga lonjezo kwa Abrahamu ndi kwa mbewu yake.”

⁴²⁰ Ndi chinthu chomwecho chimene chiri ndi ife. Kotero ngati inu muli okufa, ndipo moyo wanu wabisika mwa Mulungu, kudzera mwa Khristu, palibe kalikonse mu dziko kangakhoze kukukhudzani inu. Tsopano, inu mukhoza kupita ndi kukachita cholakwika, koma ngati inu muli kwenikweni, moonu, mwana wa Mulungu, ndipo inu mwawona kuti inu mwapanga, inu muwuka ndi kuyesa kachiwiri. Ndiko kulondola, ndipo inu simungokhala pamenepo.

⁴²¹ Koma ngati inu muli wamantha, ngati inu muli chisoso, ngati umo mulibe “uka apo” mwa inu, inu muti, “Aha, chabwino, panalibe kanthu kalikonse kwa Izo, mulimonse.”

⁴²² Ufumu wa Mulungu uli ngati munthu yemwe anatenga ukonde ndipo anapita ku nyanja, anauponya iwo umo. Pamene iye ankabwera, iye anali ndi akamba, achule, njoka, abuluzi, akangaude, ndi nsomba. Uwo ndi Uthenga pamene Iwo ulalikidwa.

⁴²³ Monga Ambuye angamuze mtumiki, monga M'bale Graham, “Pita apa *kuno*. Pita pa ngodya *iyi* ndi kukawedza kanthawi pang'ono, M'bale Graham.” Chabwino, nkutenga ukonde wake ndi kupita kumeneko ndi kuyamba kukunkha.

“Inu mukupita kuti, M'bale Bill?”

“Ine ndikupita uko kwinakwake, ndi ndikukaponya pa ngodya *iyi*.”

⁴²⁴ Ine ndikukoka, “Ndi awatu apa, Ambuye, Inu mukudziwa chomwe iwo ali.” Ine ndikoka ukondewu kachiwiri, “Chabwino, ndi awatu apa, Ambuye.”

425 Tsopano, kamba anali kamba, pa kuyamba nazo. Iwe unangogwidwa mu ukondewo. Ndiko kulondola. Ndipo umo ndi momwe anthu amagwidwira umo mwa zotengeka, “O Aleluya! Aleluya! Ambuye alemekezeke. Ulemerero kwa Mulungu. Aleluya!” Iwo angogwidwa mu ukondewo, ndizo zonse.

426 Ngati mzimu wa Kamba wakale uwo uli mwa iwo, izo sizitenga motalika, iwo ati, “Chabwino, ine ndikukuuzani inu, . . .” Apa iye akupita, akukwawa chobwerera.

427 Ndipo dona wakale Nsomba yokwawa iti, “Koma ine sindikukhoza kumvetsa basi Zimenezo.” Mukuona?

428 Abiti Kangaude akhala pamenepo kanthawi pang’ono, iwo apita “phofu, phofu, phofu,” kubwerera kumene, “Chabwino, munalibe kanthu mwa Iwo, mulimonsebe.”

429 Abiti Serpenti ati, “O, iwo ndi gulu la oyera-odzigidubuzwa. Izo basi zonse zomwe ziri kwa Iwo. Iwo ndipita komwe iwo ali ndi lingaliro labwinoko kuposa izo.” Pakuti, iwe ndi njoka, pa kuyamba pomwe. Ukonde wa Uthenga unangokugwira iwe, ndizo zonse.

430 Koma nsomba imatengedwera ku gome la Mbuye. Iye anali nsomba, pa kuyamba pomwe. Mbewu ya iye inali nsomba. Iye anayamba, nsomba, ndipo Mulungu akuzidziwa nsomba Zake kuchokera ku maziko a dziko. Aleluya!

431 Kumbukirani, izo zonse zikupuma madzi amatope omwewo, kunja uko. Izo zonse zikupuma kuchokera mu kachikhulupiriro komweko. Ndiko kulondola. “Ife tonse tinapangidwa . . . tikumwa mu Thanthwe lauzimu lomwelo. Onse anali kudya mana mu chipululu.” Kalebu ndi Yoswa ankadya mana omwewo a—amene onse a iwo ankawadya. Ndipo iwo onse anagwera mu chipululu. Koma apo panali awiri anasankhidwa kuti apite mooloka, ndipo iwo anapita mooloka. Ndiko kulondola.

432 “Ife tonse tinapangitsidwa kuti tizimwa kuchokera mu Kasupe yemweyu.” Koma si onse omwe akumwa ali kupulumutsidwa. Ife tonse tapangidwa kuti tizifuula palimodzi. Ife tonse tapangidwa kuti tizisangalala palimodzi. Koma Osankhidwa ndiwo opulumutsidwa. Kodi inu munazidziwa? Ilo linati, “Mizimu iwiri, mu masiku otsiriza, idzakhala yofanana kwambiri mpaka iyo ikanadzawanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheka,” *ngati* nkotheka. Mukuona? Uwo ndiwo Mzimu weniweni wa Mulungu, wosankhidwira ku Moyo Wamuyaya.

433 Tsopano ife tikutseka. Ndiye M’bale Neville adzazitenga kuchokera pamene ine ndikulekezerapo apa. Chabwino.

Ndipo ichi ndikunena, kuti pangano, limene linatsimikizidwira pamaso pa Mulungu mwa Khristu, lamulo, lomwe linali zaka mazana anai, zaka mazana anai ndi makumi atatu pambuyo pake, silingakhoze

kulepheretsa, kuti lipange lonjezo kukhala lopanda ntchito.

Ndilo lonjezo limene Mulungu anampatsa Abrahamu, lamulolo lisanabwere konse pokhalapo.

Pakuti ng... pakuti ngati cholandira chikhala cha lamulo, icho sichiri aponso cha lonjezo: koma Mulungu anapereka icho kwa Abrahamu mwa lonjezo.

Osati ndi chinachake chimene iwe uchita, osati mwa malamulo ena aliwonse, malamulo ena aliwonse a mpingo wanu, mwa kujowina mpingo, kapena lamulo lina lirilonse. Ichu chiri mwamtheradi kachitidwe ka chisomo cha Mulungu, kwa inu. Ndi inu apo.

⁴³⁴ Yang'anani.

Chifukwa chake ndiye kodi tizitumikira lamulo? Ilo linawonjezedwerapo chifukwa cha kulakwira, mpaka mbewu ikadze kwa iye yemwe lonjezo linapangidwirako;...

Kodi izo si zomveka basi monga mphuno pa nkhope yanga? “Ilo linawonjezedwerapo, kuti lizitumikira mpaka Mbewu itadza, yomwe inali Khristu, kwa Yemwe lonjezolo linapangidwira.”

...ndipo izo zinadzozedwera ndi angelo ndi mu manja a wokhalira pakati.

Tsopano wokhalira pakati si wokhalira pakati wa mmodzi, koma Mulungu ali mmodzi.

⁴³⁵ Tsopano, ine ndilekezera kuchokera apa pomwe, kuyambira apo pomwe kwa M'bale Neville, za Lachitatu likudza ili.

⁴³⁶ Tsopano kodi inu mukumvetsa zomwe ife tanenazi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kutu ziri mwamtheradi zosatheka kuti Mkhristu wobadwa-kachiwiri yemwe... Ine sindikutanthauza, tsopano, iye akudzitcha yekha, “wobadwa-kachiwiri.” Ine ndikutanthauza, Mkhristu wobadwa kachiwiri kwenikweni, kuti angagwe konse kuchokera ku chisomo, iye sangakhoze kuchita izo. Iye akhoza kugwa, ndiko kulondola, koma iye sangathe, konse, kuchoka pa chisomo chimenecho.

Abrahamu anagwa kuchokera pa chisomo. Zedi, iye anatero. Mulungu anamuza iye kuti “akhale kumeneko.” Iye anachoka kumeneko, koma iye sanataye konse pangano lake. Iye anali akadali wosankhidwa wa Mulungu. Iye anali mneneri ali kumeneko. Iye nthawizonse anali. Iye nthawizonse adzakhala ali Mulungu.

⁴³⁷ Tsopano zindikirani. Baibulo linanena, kuti, “Israeli yense adzapulumutsidwa.” Ndi angati akudziwa zimenezo? Baibulo linati, “Israeli yense adzapulumutsidwa.” Tsopano, “Israeli si Israeli yemwe ali wathupi, koma Israeli wa Mzimu, pakuti

mphatso ndi maitanidwe ziri zopanda kulapa.” Kodi ndi zomwe Baibulo linanena, ndime yotsatira yomwe? Agalatia. Chabwino. “Israeli yense adzapulumuka. Aliyense wa iwo ali wopulumutsidwa.” Ife timakhala bwanji Israeli? “Pokhala akufa mwa Khristu, timatengapo Mbewu ya Abrahamu, ndipo ndife olandira molingana ndi lonjezo.”

438 Paulo anati, “Iye yemwe ali wakunja si Myuda, koma iye yemwe ali mkatimo, ndiye Myuda, Iwo olonjezedwawo.” Ndipo ife tiri Mbewu ya Abrahamu, mwa lonjezo, kudzera mwa Khristu, tinamuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wathu wathu.

439 O, ine ndikuyembekeza inu mukuziwona izo. Ine ndikuyembekeza inu mukuzimvetisa izo, ngati inu mungati mukhalebe ndi Izo kanthawi pang’ono. Tsopano cha apa ife titsiriza izi, ndiye ife tiyamba pa Melkizedeki, zomwe zimabweretsanso izi kachiwiri. Ife tiyambira mobwereza pa . . . O, Izo basi, chinthu chonsecho ndi chodabwitsa. Koma ife tikungopitirira kulowa mu zinthu zonona izo.

440 Tsopano, onani, ngati inu mutatenga Ichi apa, zikuwoneka ngati, ngati inu mungathe kuwerenga Izo basi kuchokera pa kuwona kwanga . . . Monga wautatu weniweni mosamalitsa, yemwe amakhulupirira kuti pali Amulungu atatu, anandiuza ine nthawi ina, kuti, “Mateyu 3 mwamtheradi amalongosola mwapayekha payekha kuti panali atatu, Anthu atatu, mu Umulungu.”

441 Ine ndinati, “Ine ndiyenera kuti ndiziwone izo.”

442 Iye anati, “Penyani.” Nditaima pa guwa ili lomwe, iye anati, “Tayang’anani apa, Mateyu 3.” Anati, “Pamene Yesu anapita apo pomwe kuchokera mmadzi, taonani, miyamba inatsegukira kwa Iye. Ndipo Iye anawona Mzimu wa Mulungu monga nkhunda. Ndipo Liwu lochokera Kumwamba likuti, ‘Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa mwa yemwe Ine ndikukondwera kwambiri.’ Ndipo apo panali atatu: Mwana pa gombe; Mzimu Woyera pakati pakepo; ndi Atate mmwambamo.”

Ine ndinati, “M’bale, Malemba sakuwerengeka *chotero*.”

“O, inde, iwo akutero.”

Ine ndinati, “Tsopano awerenge Iwo kachiwiri, peza ngati Iwo akutero.”

443 Tsopano, chithunzi chake ndi ichi. *Apa* pali Mulungu, Mwana; *apo* pali Mulungu, Atate; *apa* pali Mulungu, Mzimu Woyera, monga nkhunda. Tsopano penyani. Baibulo linati, pamene Yesu anabatizidwa, “Mwanayo anatuluka apo pomwe mmadzi, onani, miyamba pamwamba pa Iye inatseguka. Ndipo Liwu likunena za . . . Iye anawona Mzimu wa Mulungu, Mzimu wa Mulungu, monga nkhunda.” Osati Munthu wina mmwamba *umo*, koma Mzimu wa Mulungu uwu unali Nkhunda yomwe inali pamwamba pa Iye. Ndipo Liwu likubwerapo, linati, “Uyu ndi

Mwana Wanga wokonedwa, mwa yemwe Ine ndikukondwera kukhalamo.” Tsopano werengani Mateyu 3 ndi kuwona ngati Ilo silikunena zimenezo. Mukuona? Osati anthu atatu, osati nkomwe.

⁴⁴⁴ Ndipo nchifukwa chake. Izi sizikunena kuti ndi kosatheka kuti munthu angabwerere konse, pamene iye wabwerera mmbuyo. Ilo silimanena zimenezo. Ilo silimanena zimenezo. Ilo limati, “Ndi kosatheka kwa munthu kuti abwerere konse kuti adzikonzenso yekha, iye atakhala konse mmenemo.” Iye sangakhoze kuchita izo.

⁴⁴⁵ Baibulo linati, “Iye amene wabadwa mwa Mulungu, samachita tchimo, pakuti iye sangakhoze kuchimwa. Pakuti mbewu ya Mulungu imakhalabe ili mwa iye, ndipo iye sangakhoze kuchimwa.” Ine ndingakhoze bwanji kumatchedwa wochimwa, pamene pali nsembe ili pamenepo yoti itenge malo anga? Ine ndingakhoze bwanji kufa, pamene imfa inalipiridwira kale kwa ine? Ine ndingakhoze bwanji kufa, pamene ine ndiri nawo Moyo Wamuyaya? Ine ndingakhoze bwanji kuchita zimenezo? Inu simungakhoze kuchita izo.

⁴⁴⁶ Ine ndingakhoze bwanji kukhala ndi chikalata cholembedwa kuchokera kwa a meya a mzinda uno, kuti ndizithamangitsa mailosi sikisite pa ora podutsa mu mzinda uno, ndipo ofesara wina aliyense nkundimanga ine pa kuthamangitsa mailosi sikisite pa ora? Inu mungachite bwanji zimenezo? Ine ndiri ndi chilolezo chochokera kwa a meya chikuti ine ndingakhoze kumachita izo. Iye sangakhoze kundimanga ine. Mpumulo w—wake. . . Iye akhoza kuwomba kherere ndi china chirichonse, ndipo ine ndikhoza kungozinyalanyaza izo. Sizikutanthauza kanthu; ine ndiri ndi chilolezo.

⁴⁴⁷ Ndipo ine ndingakhoze bwanji, ndiye, Khristu atandifera ine kale ndipo ine nditakhala chilungamo Chake chifukwa cha chisomo Chake ndi chikondi kwa ine? Ine ndingakhoze bwanji kuchimwa, pamene pali chinachake chiri pakati pa ine ndi Mulungu, nsembe? Ine sindingakhoze kuchimwa. Sindingakhoze kuchita izo. Mulungu samandiwona konse ine; Iye amamuwona Khristu. Iye akuima mmalo mwanga. Ndipo pamene ine ndichita chirichonse cholakwika, Khristu amatenga malo anga. Ine ndinapanga chivomerezo changa, “Ndine wolakwa, Iye ndi wolondola. Ambuye, Inu mukuwudziwa mtima wanga. Inu mukudziwa ngati ine ndikutanthauza izo kapena ayi. Ndipo ine ndine wolakwa. Ndikhululukireni ine.” Mulungu samaziwona konse izo. Magazi a Yesu amandiphimba ine, nthawi zonse. Ndiye Mulungu angathe bwanji kundiwona ine? Tchimo lingakhoze bwanji k—kukhala likuwerengedwera kwa ine, pamene Iye sangakhoze kuchita izo? Basi mwamsanga pamene ine ndichita izo, izo zimakhululukidwa. [M'bale Branham akusisita chala chake—Mkonzi.] Ndiko kulondola.

448 Ziri monga kutenga—kadontho kakang’ono monga *aka*, kodonthotsera mdiso kakang’ono, ndi kukatenga kodzaza kapezi wakuda ndi kumugwirizira iye pamwamba pa nsambidwe ya bulichi, ndi kungomugwetsera iye mmenemo, ndiyeno yeserani kumupeza iye kachiwiri. Iye amangosanduka bulichi. Kapeziyo amasanduka bulichi. Ndipo izo ndi zomwe, machimo anu olapidwa, ngati inu muli mwa Khristu. Pakati pa inu ndi Mulungu pali nsambidwe yonse ya bulichi, ndipo tchimo lanu limakhala lolungama chifukwa Nsembe yolungama ikukudikirirani inu pamenepo.

Nkadzafika pa mtsinje pakutha tsiku,
Mphepo ya chisoni itawomba;
Lingaliro lokondwetsa mtima wanga,
Sindzawoloka Yordani ndekha.

449 Ndicho chinthu chimodzi chabwino. Ndicho chinthu chimodzi chabwino. Ine sindidzasowa kuwuoloka iwo. Limodzi la masiku awa, ife tikubwera ku mapeto a msewu. Dzuwa lidzakana kuti liwale, ndiye Mulungu adzaitana.

450 Adamu adzafikira ndi kumugwedeza Eva, nkuti, “Wokonedwa, ndi izi apa. Ndi nthawi yoti tiwuke.”

451 Eva adzafikira ndipo adzamugwira Abele, nkuti, “Tulukamo, wokonedwa. Ndi nthawi yoti tiwuke.” Abele adzamugwira Seti. Ndipo Seti adzamugwira Nowa. Nowa adzamugwira . . . O, mpaka mmusi, mpaka mmusi kwa Abrahamu, ndi mmusi pamene iwo akubwera. Padzakhala pali kugwedeza kwakukulu ndi kudzutsa pamene Mwana wa Mulungu azibwera. Ife tidzaima mwa mafananidwe Ake pa tsiku limenelo.

452 Tsopano, ngati inu muchita tchimo kuno, inu mulipirira pa ilo. Ine . . .

453 Zikupitirira kubwera basi mu malingaliro anga, ine ndiyenera basi kuti ndizinene izo. Ine ndayesera kuzitonholetsa izo, nthawi zinai kapena zisanu. Ine ndiyenera kuti ndizinene izo. Ndi angati akumukumbukira m’bale uyu, m’busa, yemwe ankakhala kuno ku mpingo wa Mulungu? M’bale, komwe kuno, dzina lake anali ndani? Ankagwira ntchito ku Vorgang kumusi uko. O, inu nonse . . . Mpingo woyamba wa Mulungu, komwe kuno pa ngodyapa. Kapena, ankagulitsa ma Rawleigh mu nthawi ya k—kusowa chuma. Mwamuna waumulungu weniweni, woyera. M’bale Smith anatenga malo ake kuntunda uko. Ine ndimutchula dzina lake mu maminiti pang’ono. Iye anali munthu wopulumutsidwa ndi Mulungu.

454 Kumbukirani, ngati inu simungayende mwa kukonzedwa, ndipo inu mukachita chinachake cholakwika ngati Mkhristu, Mulungu azikuchenjezani inu. Ndiyeno ngati inu simutenga kuchenjezako, Iye angokuchotsani inu pa dziko lapansi pomwepa. Ndi chimene Iye anachita.

455 Inu mukukumbukira, mu Baibulo? Yang'anani pa mpingo wa Chikorinto uja. Iye anawauza iwo chomwe iwo anali, mwapamalo, mwa Khristu. Koma iye anawachenjeza iwo za chomwe chikanati chichitike. Ndipo iwo anadzikonza okha, anawongoledwa, ndi Mulungu.

456 Ndipo m'bale wamng'ono uyu, iye anali m'bale wamng'ono wodabwitsa, ine ndikukhulupirira, munthu wopulumutsidwa ndi Mulungu. Ndipo iye anadzipezera ntchito kumusi kuno k... ku Vorgang. Ngati ena a abale ake ali pano, ine ndikuyembekeza inu simukuganiza kuti i...Ine sindikukudziwani inu ngati muli pano. Koma, Ramsey, M'bale Ramsey, ndi angati akumukumbukira M'bale Ramsey kuno ku mpingo wa Mulungu? Zedi, inu muli, mwamuna wamng'ono wodabwitsa. Ndipo iye ankakonda kubwera ku nyumba yanga ndipo ife tinkayankhula palimodzi, ndipo ife tinkakhala pamenepo ndi kumalira ndi kugwirana dzanja la wina ndi mzake; Mkhristu weniweni.

457 Tsiku lina ine ndinapita mmenemo kumusi uko, nditangobwera kumene kuchokera kutsidya kwa nyanja ku msonkhano, ndinali ndi galimoto yanga ikufufuzidwa, M'bale Ramsey anati, "Kodi ine ndikuchitire chiani iwe, Billy?"

458 Ine ndinati, "Ifufuze iyo, M'bale Ramsey. Uyisinthe mafuta."

459 "Chabwino," iye anati, "chabwino, wokondedwa." Anati, "Inu munali ndi msonkhano wabwino?"

460 Ine ndinati, "O, M'bale Ramsey, uwo unali wodabwitsa." Ine ndinati, "Ine ndikukhumba iwe ukanadzapita nane nthawi ina. Bwanji iwe sumamapita ndi ine?"

Iye anati, "Ine sindikuwatumikira Ambuye panonso, Billy."

Ine ndinayang'ana pozungulira, ine ndinati, "Iwe ukuti chiani?"

461 Iye anakhala ngati akuti, "Ine sindimamutumikira Iye panonso," anayenda nachokapo.

462 Ine ndinaganiza, "O, iye akungopitirira." Ine ndinapitirira, ndinapita kwinakwake.

463 Ndinabwerera ndipo ndinadzalowa mu galimoto yanga. Ine ndinadzafika kunyumba. Ine ndinayamba kuganiza za izo, "Ine sindikuwatumikira Ambuye panonso."

464 Ambuye anachiika icho pa mtima wanga kuti ndibwerere ndi kukamufunsa iye kachiwiri. Chotero, ine ndinati, "Meda, zisamalira zinthu."

465 Ndipo ine ndinalowa umo, ndipo ndinalowa mu galimoto yanga ndipo ndinabwererakonso, ndinaimako kachiwiri, ndinalowa mu Vorgang. Ine ndinati, "M'bale Ramsey, ine ndikufuna kuti ndikufunse iwe funso."

Anati, "Chabwino, Billy, ndi chiani ilo?"

Ine ndinati, “Iwe unanena, kanthawi kapitako, iwe sukuwatumikira Ambuye panonso. Iwe umangondiseleula ine, sichoncho iwe?”

Iye anati, “Ayi.”

Ine ndinati, “M’bale Ramsey, i—iwe sukutanthauza zimenezo.”

Iye anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Kodi iwe sukumukonda Iye?”

Iye anati, “Ngati ine ndikanamamukonda Iye, ine ndikanati ndizimutumikira Iye. Sichoncho ine, Billy?” anayenda nachokapo.

Ine ndinaganiza. “Tanena, M’bale Ramsey!”

Anati, “Ine sindikufuna kuyankhula zinanso za izo.”

⁴⁶⁶ Ine ndinapita kunyumba, ndinalowa mu chipinda, ndinatseka chitseko. Ndipo, o, inu mukudziwa momwe iwe umamverera kulemedwa kwenikweni, ngati iwe unamulanda mwana mabisiketi kapena chinachake, inu mukudziwa. I—ine ndinaganiza, “Chiani? Sizingakhale chomwecho. Ndithudi chinachake chachitika kwa M’bale Ramsey.”

⁴⁶⁷ Ndipo kuli mnyamata wamng’ono wachikuda, dzina lake Jimmy, iye amabwera kuno ku mpingo. Ali ndi mwendo umodzi, inu mukudziwa; iye amatsimphina, monga ngati. Ine ndaiwala dzina lake, amagwira ntchito uko ku Vorgang, amayendetsa chophwasulira. Iye anakomana nane, ndipo iye anati, “Inu mukudziwa, Abusa a Branham,” iye anati, “Ine sindikudziwa izi za Dr. Ramsey uyu kuno.” Iye anati, “Ine ndinamuza iye, tsiku lina, anati, ‘Ife tonse tikuchita mantha ngakhale kuti titsegule kamwa yathu kunoko.’ Ndinati, ‘Inu munali munthu waumulungu.’ Koma,” anati, “Iye anatenga chikalata chake cha ulaliki ndipo anapita ku dengu ndipo anakazing’amba izo, ndipo anaziponyera izo mu dengulo, anati, ‘Ine sindikufuna kanthu kochita ndi izi panonso.’”

Iye anati, “Hei, bambo!” Ndinati, “Inu simukuyenera kuchita zimenezo.”

Iye anati, “O, Jim, ine ndathana nazo zotumikira Ambuye.”

Chotero iye anapitirira, anati, “Inu simukutanthauza zimenezo.”

⁴⁶⁸ Ndipo anati, “Ndiye iye anandiiza ine, anati iye amabwera kuti adzapale mavalavu ake, pa Tsiku Laapantchito,” ine ndikukhulupirira ilo linali. “Ndipo iye anati, ‘Tsapano, ine ndikufuna kuti iwe ubwere udzandithandize ine, Jim.’”

⁴⁶⁹ Iye anati, “Ine ndidzakuthandizani inu ndikabwera kaye kuchokera ku tchalitchi, koma choyamba ine ndikupita ku tchalitchi.”

⁴⁷⁰ Anati iye anabwerera uko, “Ndipo Bambo Ramsey anali akupala mavalavu pa galimoto yawo. Iye anati, ‘Jimmy, tapita kaye ku mtsinjeko. Malo ogulitsira mowa awatseka kuno. Tapita kaye ku mtsinjeko ndi kukanditengera ine mpukutu wa mowa.’”

⁴⁷¹ Iye anati, “Bambo Ramsey, ine ndakhala wolakwa mu zinthu zambiri, koma ine sindidzakhala konse wolakwa pomutengera wantchito wa Ambuye mpukutu wa mowa.” Iye anati, “Ayi, bwana. Ine sindichita konse zimenezo.”

⁴⁷² Ndipo iye anati, “Chabwino, tiye pita. Kandigulire iwo, Jim.”

⁴⁷³ Iye anati, “Bambo Ramsey, ine ndipekesa mavalavu anu. Koma ngati inu muti mugule mowa uliwonse, inu pitani mukaugule uwo nokha.” Iye anati, “Ine sindingati ndikamugulire konse wantchito wa Ambuye chinachake chonga izo.”

⁴⁷⁴ Chotero Ramsey analumphira mu galimoto ya Jimmy, anawoloka mtsinjewo, anabwerera, ataledzera mwatheka, ali ndi mpukutu wa mowa, akuumwa iwo.

⁴⁷⁵ Iye anayamba kupita pansi, ndipo anayamba kudwala. Mukuona? Mulungu sakanakhoza kuyankhula kwa iye. Ine ndinamuchenjeza iye, ine ndinachita chirichonse chimene ine ndikanakhoza. M'bale Smith anapita kwa iye ndipo anakamuchenjeza iye. Aliyense anayesera kuchita chirichonse chimene iwo akanakhoza kuchita kwa iye. Komabe, iye ankangogwedeza mutu wake. Chinachitika ndi chiani? Iye anayamba kudwala ndipo anafa. Izo zikusonyeza kuti iye anali munthu wopulumutsidwa. Ngati Mulungu sakanakhoza kumupangitsa iye...kumubweretsa iye pa kumvera, Iye anayenera kuti amuchotse iye pa dziko lapansi ndi kumubweretsa iye Kwathu. Ndizo ndendende zomwe Baibulo linanena. Ndi zomwe Baibulo linalonjeza. Ngati inu simungakhoze kulandira kukonzedwa, inu muyenera kuti muzibwera Kwathuko.

⁴⁷⁶ Chotero Mulungu sangakhoze kukutayani inu Iye atakupulumutsani inu kale, koma Iye akhoza kufupikitsa masiku anu kuno, ndi kukupangitsani inu kulipira pa tchimo lililonse lomwe inu mwalichita. Chotero, ngati inu muchimwa, inu mudzayenera kuti mulipire pa zomwe inu munazichita. Muzingokumbukira zimenezo.

⁴⁷⁷ Tsopano, tsopano Ambuye akhale ndi inu. Ine ndikukhulupirira, usikuuno, kuti M'bale Ramsey anali wopulumutsidwa. Mwamtheradi, ine ndikukhulupirira zimenezo. Koma iye sankafuna basi kumumvera Mulungu, ndipo pamene iye sankafuna kumumvera Mulungu, Mulungu amayenera kuti amubweretse iye Kwawo. Ndi chinthu chokha choti angachite, chifukwa, kodi icho chinali chiani? “Iye akanabweretsa chitonzo ndi manyazi kwa Magazi omwe iye

anayeretsedwa nawo.” Uko nkulondola? “Ndi kuwerengera panganollo ngati chinthu chosayera,” ngati izo siziri ndendende chomwe kalata ya kwa Ahebri iyi inanena. Mukuona? Izo zikanakhala zosatheka kuti iye ataike, koma iye akanabweretsa manyazi ndi chitongo, chotero Mulungu anayenera kumuchotsa iye pa dziko lapansi ndi kumubweretsa iye Kwawo. Ndizo ndendende zomwe zinachitika.

Tsopano Ambuye akudalitseni, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu kwa mphindi yokha ya pemphero.

⁴⁷⁸ Tsopano, Atate woyera kwambiri ndi achisomo, ife ndithudi tiri oyamikira kwa Inu pa lonjezo lomwe ife tiri nalo, kuti Inu simudzatisiya konse ife kapena kutitaya ife. Inu munalonjeza kuti Inu mudzapita limodzi nafe kupyola mmoyo, ndipo mu imfa Inu mudzakhala pafupi nafe. Inu munatilonjeza ife kuti ife tinali nawo Moyo Wamuyaya. Inu munaupereka Iwo kwa ife mwaulere. Ife sitingakhoze konse kuwutaya Iwo. “Onse omwe adza kwa Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya.” Ndipo ngati iwo uli Moyo Wamuyaya, Iwo ulibe mapeto, ndipo Inu munalonjeza kuti mudzatiukitsa ife mu tsiku lotsiriza. Kwa ichi ife tiri oyamikira kwambiri. Ife tiri othokoza kwambiri kuti Mawu Anu amatiphunzitsa ife izi. Izo zimatipatsa ife chiyembekezo chotsimikizika. Izo zimatipangitsa ife kudziwa kuti Atate athu ali Achikondi. Iye amatikonda ife, ndipo Iye anatisankha ife. Inu munati, “Inu simunandisankhe Ine, koma Ine ndinakusankhani inu ndipo ndinakudzozani inu.” Ndipo ine ndikukuthokozani Inu, Atate, kuti Inu munachita chotero. Ndipo ambiri ali pano, usikuuno, ndi omwe anadzozedwera ku Moyo Wamuyaya, ndipo amulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wawo wawo. Ndipo zipatso za Mzimu zikutsatira moyo wawo: oleza, ofatsa, odzichepetsa, chikondi, chimwemwe, mtendere kupirira motalika, ubwino. Ife tiri othokoza kwambiri chifukwa cha izo.

⁴⁷⁹ Ndipo ife tikupemphera, Atate, kuti ngati pali ena pano, usikuuno, omwe alibe zipatso zimenezo kuti ziziwatsatira iwo, koma iwo akudalira pa zododometsa zina, chifukwa iwo anali atatengeka, tsiku lina, chifukwa iwo anafika pochititsidwa zina, iwo anamverera bwino, iwo mwina anafuula, iwo mwina anachita zinthu zambiri. Koma, Atate, ngati iwo alibe chipatso cha Mzimu, chimene chimawasunga iwo tsiku ndi tsiku mu chikondi chowirikiza, kuwakhululukira adani awo, kukonza zolakwitsa zawo, ndi kumakhala mwamtendere ndi kukonda, ndi mokoma ndi achifundo kwa wina ndi mzake, ndi odzipereka kwa Mpingo, chikondi kwa Khristu ndi kwa ana Ake, O Mulungu Wamuyaya, akhululukireni iwo. Ngakhale iwo ali ziwalo za mpingowu, ziwalo za thupi la padziko, mulole iwo apite tsopano ndipo akaike kumbali ntchito zachithupithupi, zakufa izo, ndipo alimbikirebe mpaka ku ungwiro. Perekani izi, Ambuye. Mulole iwo abwere kwa Mmodzi wangwiroyo ndi kumulandira Iye ngati

chitetezero cha machimo awo, kuti Iye akhoze kuimira monga nsembe yangwiro kwa bambo wochimwa ndi mayi wochimwa. Ndipo apatseni iwo chisomo Chake cha chikondi ndi mtendere, mpaka iwo afike mu Kukhalapo kwa Mulungu kuti akhale moyo kwanthawizonse. Perekani izi, Atate.

Pamene ife tiri chiweramire mitu yathu:

⁴⁸⁰ Ngati alipo mmodzi woteroyo yemwe angafune kuti asinthanitse moyo wachithupithupi wa miyambo, ya maubatizo, ya zomverera, ya zinthu zazing’ono zachithupithupi zonga izo, akufuna mtima weniweni wodzala ndi chikondi chenicheni, k—kuti iwe ukhoza kuyenda nkupita kwa mdani wako wowawitsa, nkuika mikono yako momukumbatira iye nkuti, “M’bale, ine ndimakupempherera iwe. Ine ndimakubonda iwe.” Ngati inu mungafune kuti musinthanitse chokuchitikirani icho cha zinthu zachithupithupi pofuna chokuchitikirani chenicheni cha chikondi, kodi inu mungakweze dzanja lanu kwa Mulungu? Ndi kuti, “Mulungu, nditengeni ine usikuuno, ndi kundipanga ine chimene ine ndiyenera kuti ndikhale ndiri.” Ine ndizikupemphererani inu, pa guwa pomwe pano. Kodi inu mungakhumbe pemphero? Kwezani manja anu.

⁴⁸¹ Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, bwana. Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Wina wakenso? Mulungu akudalitseni inu, bwana. “Ine ndakhala ndiri mu mpingo kwa zaka.” Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu apa, m’bale. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, dona wamng’ono. “Ine ndimupempha Mulungu kuti andipange ine wamtendere.” Mukutero inu... Kodi inu mukututuma kwenikweni? Kodi inu mwachoka mu zoyenera? Kodi inu mukukaikira? Kodi inu mukukankhidwira uku ndi uko? Kodi inu mukudabwa ngati Izo ziri zolondola kwenikweni kapena ayi? Pamene inu mukubwera kwa Khristu, kodi inu mukumabwera ndi chitsimikiziro chathunthu, mtima wodzaza ndi chikondi? Kodi inu mukuyenda kufika kwa Iye wopanda mantha amodzi, mukuti, “Ine ndikudziwa Iye ndi Atate anga”?

⁴⁸² Ndipo palibe kutsutsidwa, inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo. Inu mukuzidziwa izo. Ndipo inu mukuzindikira moyo wanu: ndinu wachikondi, ndinu wokhululukira, ndinu woleza, ndinu wamtendere, ndinu wofatsa. Zipatso zonse izi za Mzimu zikutsagana ndi moyo wanu, tsiku ndi tsiku. Ndipo mwamsanga pamene inu muchita chirichonse molakwika, “O, mai.” Basi mwamsanga pamene izo zifika ku malingaliro anu, “inu mwalakwitsa,” mwamsanga inu mumazikonza izo, apo pomwe. Musati muzidikirira miniti ina, kupita apo pomwe ndi kukazikonza izo. Ngati inu simutero, chabwino, inu mulibe Mzimu wa Khristu. Inu mukhoza kukhala mkazi wabwino, inu mukhoza kukhala bambo wabwino, inu mukhoza kukhala woganiziridwa bwino mu mpingo, inu mukhoza kukhala woganiziridwa bwino mwa oyandikana nawo,

koma kodi inu munapita mpaka ku ungiro uwo, ku malo awo pomwe inu mukudalira mwathunthu mwa Khristu? Ndipo mwa izi, nkukupatsani inu chisindikizo. “Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo kunawerengedwa kwa iye ngati chirungamo. Ndiye Mulungu anamupatsa iye chisindikizo cha mdulidwe, ngati chitsimikiziro.”

⁴⁸³ Tsopano inu mukuti, “Ine ndikukhulupirira Mulungu. Ine ndinapanga chivomerezo.” Koma kodi Mulungu anakupatsani inu chisindikizo cha Mzimu Woyera, kubweranso pa moyo wanu, cha chikondi, chimwemwe, zipatso za Mzimu, kuti zizitsimikizira kuti inu munapululumutsidwa? Ngati Iye sanachite zimenezo, ndiye Iye sanachizindikire chikhulupiriro chanu panobe. Inu mwangopanga chivomerezo. Iye sanachilandire icho, pali chinachake cholakwika. Kodi inu mungakonde kuti mumulandire Iye, ndiye? Kwezani dzanja lanu, ngati alipo winanso, ife tisanapemphere.

⁴⁸⁴ Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, nanunso. Mulungu akudalitseni inu. Chabwino. Wina wakenso, ife tisanati tipemphere? Chabwino. Mulungu akudalitseni inu, kumbuyo uko, mlongo. Mulungu akudalitseni, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, m’bale wanga. Ndiko kulondola. Manja ena khumi, manja khumi ndi asanu akhala ali mmwamba.

Tsopano tiyeni tipemphere.

⁴⁸⁵ Ambuye wodala, pa mpando wawo, iwo apeza guwa. Ndi pa mpando wawo, pomwe iwo akhala tsopano, pomwe Inu mwayankhula kwa mitima yawo, kuti iwo “ali kulakwitsa.” Ndi pa mpando pawopo pamene Inu mwaika chikhumbo mu mtima mwawo, kuti iwo “akukhumba kukhala mochuluka monga Yesu.”

⁴⁸⁶ Iwo akufuna moyo wawo kuti usinthidwe. Iwo akufuna kuti akhale oleza ndi odzichepetsa. Iwo akufuna kuti akhale aulemu ndi odzaza chipiriro. Iwo akufuna kuti akhale opirira-motalika, oleza. Iwo akufuna kuti akhale kwambiri monga Mkristu, ofanana ndi Khristu, mpaka dziko liziti, pamene iwo akuyenda mu msewu, “Bambo uyo ndi Mkristu weniweni. Mkazi uyo ndi Mkristu weniweni. O, iwo ndi anthu aulemu kwambiri, ofatsa, okoma kwambiri!”

⁴⁸⁷ Perekani izi, Ambuye, kuti iwo alandire chowachitikira icho, usikuuno. Ndipo mulole iwo asatsamire konse pa kukhoza kwa mpingo wawo, pa kuchitira kwawo limodzi ndi mpingo wina uliwonse, chipembedzo china chirichonse; kapena ngakhale osati pa zomverera zawo, pa zododometsa zirizonse, monga ngati motengeka, chinachake chimene chinachitika; mwina iwo anafuula, anayankhula mu malirime, kapena chinachakenso.

488 O Mulungu Wamuyaya, mulole iwo asayesere kudalira kuti apita Kumwamba pa zimenezo, pakuti ife tikuziwona izo nthawi zochulukana kwambiri zikulephera momvetsa chisoni. Ndipo Inu munati izo zikanadzalephera, “Ngakhale ali malirime, iwo adzaleka! Pamene pali mauneneri, iwo adzasowa. Pamene pali chidziwitso, icho chidzasowa. O, zinthu zonse izi, kapena ngakhale mphatso, zozizwitsa za machiritso, izo zonse zidzathetsedwa. Chikondi Chaumulungu chokha icho chidzakhalapobe.”

489 Mulungu, lengani izo mu mtima mwawo, ndi kuwalola iwo adziwe kuti uwo ndi Mzimu umene umabweretsapo zipatso. Chitani izo pakali pano, Ambuye, pamene ife tikuyembekezera pa Inu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

490 [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] Mipira ya moto ikuwuluka, ndi kuwona njiwa zikuwuluka mmbuyo ndi mtsogolo kudutsa mchipindachi, kumuwona Khristu akubwera ali ndi minga mmanja Ake, ndi Mwake. . . O, kodi inu mukudziwa kuti ilo ndi khwekhwe la wotsutsakhristu? Iye anati, “Pamene zinthu izi zidzayamba kuchitika, ndiye muzidzayang’ana mmwamba, chiwombolo chanu chikuyandikira.” Ndiye icho nchifukwa ine ndikuyesera kukanikizira miniti iliyonse yomwe ine ndingathe kwa mpingo, ndi kukupangitsani inu kukhala olimba. M’bale Neville mwina nthawizonse sangamakhale ali ndi ife. Ine ndikukhulupirira M’bale Neville kuti ndi mphunzitsi wabwino, wolama wa Uthenga. Ife sitikudziwa chomwe chidzatsirizire njira yake kwa guwa ili, ndipo, pamene icho chiti chidzabwere apa, “Nkhosa Zanga zimalidziwa Liwu Langa.” Mukhale ndi Mawu awo. Musati mudzawasiye konse Mawu amenewo. Inu mudzakhale kumene ndi Iwo. Inu muziima molimba mu ufulu womwe Khristu wakupangitsani inu kukhala mfulu. Musati mukhale omangidwa mu magoli onse awo a ukapolo ndi zina zotero. Imani molimba, ndi kuima mfulu. Mulungu azikudalitsani inu. Ife tiribe kanthu mu dzikoli koti tizikawopa.

491 Inu nthawizonse mumadabwa. Ine ndimazindikira anthu amabwera kuti adzapemphereredwe, iwo amangosunthira mu mzere. Nthawi yotsatira iwo akawona msonkhano wa machiritso, iwo amadzapita mu mzere *uwu*, iwo adzapita mu mzere *uwu*. Ine sindikuwatsutsa iwo. Iwo akuyesera kuti apeze chitonthozo, koma iwo akupita mwa njira yolakwika. Inu mukuchita mosemphanitsa, zomwe Mulungu anati musamachite. Mukuona? Pamene inu muyenda molimba mtima kupita ku Mpandowachifumu wa chisomo, ndi kukhulupirira, kuti, “Inu mwapempha, inu muzilandira.” Khalani ndi Icho. Umo ndi momwe izo zimachitidwira; osati kumangolumphika kuchokera ku mishoni kupita ku mishoni, kuchokera ku mpingo kupita ku mpingo, kuchokera ku msonkhano wokopa kupita ku msonkhano wokopa.

492 Pakuti, iwo apangitsa misonkhano ya machiritso iyi ngati mulu wa zachabechabe. Ndithudi, iwo atero. Izo zafika pa malo pamene, anthu aluntha, iwo amayang'ana apo ndipo iwo amadabwa kuti zonsezi ndi chiani. Apo, Mulungu samafuna zinthu zimenezo. Machiritso samasowa kuti azikhala mmisonkhano yokopa. Machiritso azikhala ali mu mpingo wamba uliwonse, mphatso zonse izi zizigwira ntchito. Koma osati muzipita kumbewu ya mphatso zimenezo. Musati muziika chidwi chirichonse kwa mphatsoyo. Ngati Mulungu akufuna kuti akugwiritseni inu ntchito kwa chinachake, Iye azichita izo. Koma, ziyang'anani motsatira Woperekayo.

493 Marteni Lutera, nthawiina atatha kuyankhula mmalirime, iye anafunsidwa chifukwa chiani iye samalalikira izo, iye anati, “Ngati ine ndikanamalalikira izo, anthu anga akanamatsatira mphatsoyo mmalo mwa Wopereka.” Ndiko kulondola.

494 Moody, nthawiina, akuyankhula, ndipo anayamba, pamene iye anali kulalikira chotero pansu pa kudzoza, iye anayankhula mu malirime. Iye anati, “Mulungu, ndikhuluulukireni ine chifukwa choyankhula mawu opusa.” Ndithudi. Mukuona? Ndipo iwo anali nazo zinthu zimenezo. Iye timazikhulupirira zinthu zimenezo, koma izo ziyenera kuti ziziikidwa mu malo ake. Ndipo izo zisati ziziikidwa ngati maumboni.

495 Palibe chinthu chimodzi chasiyidwa mu Baibulo, ngati “umboni wa Mzimu Woyera,” zipatso zokha za Mzimu. Kapezeni malo ena aliwonse omwe Yesu ananena chomwecho. Inde, bwana. Umboni wa Mzimu Woyera ndi chipatso cha Mzimu. Yesu ananena chomwecho, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” “Ndipo chipatso cha Mzimu ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira, ubwino, mtendere, kuleza, kufatsa. Ndipo chipatso cha mdani ndi udani, madano, njiru, ndewu, ndi zina zotero; ndizo chipatso cha mdani.” Chotero, inu mukhoza kuweruza mwa njira yomwe inu mukukhalira, pamene inu mwayima ndi Mulungu. Ngati mtima wanu wonse uli mu chikondi ndi Iye, ndipo inu mukumukonda Iye ndipo ndinu woleza, ndipo mukumakhala ndi Iye tsiku lililonse, inu mudziwa inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo. Ngati izo siziri, ndipo inu muli mwa mtundu wina, inu mukungosanzira Chikhristu. Ndiko kulondola. Chimene, kusanzira konse kwa chithupithupi ndithudi kudzayalutsidwa. Iye tikudziwa izo.

496 Chotero, musati muzikhala mtundu wa moyo umenewo, inu simukusowa kuti muzitero. Nchifukwa chiani inu mungati muzivomereza choloweza mmalo, pamene mlengalenga monse mwadzaza ndi zabwino ndi zenizeni? Ndithudi. Mundirole ine nditenge Mulungu, Icho ndi chimene ine ndikuchifuna. Amen.

497 Tsopano, kodi aliyense anabwera kuti adzapemphereredwe? Ngati inu munatero, kwezani dzanja lanu. Iye tinali ndi msonkhano wa machiritso mmawawu. Ine ndikulingalira

ndiye... Dona uyu apa? Chabwino, mlongo, kodi inu mungabwere patsogolo ndiye? Ndipo m'bale wathu, mkulu, pano, bwerani tsopano kudzawadzoza.

[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]

. . . walani pa ine;

O, walani pa ine, Ambuye, walani pa ine,
Kuwala kwa ku nyumba ya kuwala kuwale pa
ine.

⁴⁹⁸ Kodi Iye si wodabwitsa? Tiyeni tingoweramitsa mitu yathu, mwakachetechete kwenikweni tsopano. Ndipo, *Walani Pa Ine*, kachiwiri. Tsopano, zibwerani apa tsopano, aliynense, yemwe, “Walani...” Zingomamupembedzani Iye mu moyo wanu tsopano, onani, khalani bata. Utumiki wa machiritso ukubwerapo. Uthenga watha. Tiyeni tizipembedza.

Kuwala kwa ku nyumba ya kuwala kuwale pa
ine;

O, walani pa ine, Ambuye, walani pa ine.
Kuwala kwa ku nyumba ya kuwala kuwale pa
ine.

Mongatu Yesu, mongatu Yesu,

O, padziko ndikhale monga Iye;
Njira ya moyo mpaka ku Ulemerero,
Ndipempha nkhalale monga Iye.

Tiyenda nkuwala, kokongola,
Mame achifundo chowala;
Kuwale usana ndi usiku,
Yesu, kuwala kwa dziko.

Oyera falitsani,
Yesu, kuwala kwa dziko;
Mabelo Akumwamba alire,
Yesu, kuwala kwa . . .

Tilandireni ife, Ambuye, pamene ife tikukupembedzani Inu.

Tiyenda nkuwala, kokongola,
Mame achifundo chowala;
Kuwale usana ndi usiku,
Yesu, kuwala kwa dziko.

⁴⁹⁹ Kodi inu simukukukonda basi kukhula uko? Inu mukumverera bwino? Kwezani dzanja lanu, munene. Pali chinachake ndi nyimbo za kachitidwe kachikale ako, nyimbo zachikale, ine kulibwino ndizikhala ndi izi kusiyana ndi nyimbo zonse zatsopano zachidziko izi zomwe zaikidwamo, ndi mu mipingo ya Chikhristu. Ine ndimakonda yachikale ija, ine ndimakonda.

Yesu, mndisunge kumtanda, (Mai!)
 Ku kasupe wofunika,
 Waulere kwa onse, mtsinje wochiza,
 Wa ku phiri la Kalvare.

Mu mtanda, mu mtanda,
 Pakhale ulemerero wanga;
 Moyo wanga ukwatulidwire
 Kutsidya la mtsinje.

500 Ine ndikanakhoza kuchoka mu dziko mophweka kwambiri pamene iyo ikuimbidwa. Sichoncho inu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kudabwitsa kwakeko! Kodi izo zonse zathetsedwa? Inu mukudziwa, ine ndikukondwa ndinazithetsa izo zonse. Sichoncho inu? [“Ameni.”] Ngongole yakale inatha, kale kale ilo. Ine ndinamuza Iye, “Ambuye, ine sindikufuna vuto lililonse ku mtsinje uko. I—ine ndikufuna ndikhale wotsimikiza tsopano.” Ine ndikufuna ndizimudziwa Iye. Ine ndikufuna ndizimudziwa Iye.

501 Kuli dzenje lalikulu, lakuda lomwe laikidwa patsogolo pa aliyense wa ife. Ife talunjika njira imeneyo. Nthawi iliyonse pamene mtima wathu ugunda, ife tikuyandikira yandikira. Koma pamene ine ndikafika kumeneko, ine sindikufuna ndizikakuwa ngati wamantha, ine ndikufuna kuti ndidzikulunge ndekha mu minjira ya chilungamo Chake, kukalowa mmenemo, podziwa ichi, kuti, “Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiukitsiro Chake.” Kutu, pamene Iye aitana, ine ndidzatuluka kuchokera pakati pa akufa. Mai!

502 *Chikhulupiriro Changa Chiri Kwa Inu*, tiyeni tiyimbe iyo tsopano.

Chikhulupiriro changa chiri kwa Inu,
 Mwanawankhosa wa Kalvare,
 Mpulumutsi Wauzimu.
 Ndimveni popempha,
 Mchotse machimo anga,
 Musalole ndisochere
 Kutali Nanu.

503 Tsopano, Mphunzitsi wamkulu, monga Inu mwatiphunzitsira ife mu Mawu Anu opambana kwambiri, mitima yathu ikungonjenjemera, ndi chisomo chokwatulitsa, podziwa kuti ife tadutsa kuchokera ku imfa tapita ku Moyo. Zonse ziri kudzera mu ubwino wa Ambuye wathu Yesu, yemwe anatiyitana ife, ndipo watitsuka ife mu Magazi Ake, ndipo watipereka ife pamaso pa Mpandowachifumu wa Mulungu, opanda cholakwika, opanda chilema, pakuti Iye anatenga machimo athu. Ife tiribe tchimo. “Mulungu anaika kusaeruzika kwa ife tonse pa Iye, ndipo Iye anavulazidwa chifukwa cha kulakwa kwathu.” O, momwe ife tikumukondera Iye, Mwanawankhosa wamkulu wa Mulungu!

⁵⁰⁴ Ndipo ife tikupemphera, Atate, kuti Inu mutipatse ife mayankhulidwe, kalongosoledwe, kuti ife tikhoze kumawauza ena; kuti iwo akhoze kumudziwa Iye, nawonso, ndi kumukonda Iye, pakuti Iye amawakonda iwo. Tipatseni ife chisomo ichi.

Ndipo zikomo Inu, Atate, chifukwa cha makanda awo obadwa kumene amene angobwera kumene mu ufumu wa Mulungu. Mulole iwo akapeze mpingo wabwino kwawo kwinakwake, ndipo kumeneko azikakutumikirani Inu mpaka imfa itawamasula iwo kuchokera ku thupi ili lakale la zopweteka ndi zowawa, ndi kuwapereka iwo pamaso pa Iye, opanda cholakwika, opanda chilema, mu m'badwo ukudzawo, ali ndi Moyo Wamuyaya. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Ameni.



BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org